# *Chododometsa*

Zikomo inu, m'bale. Zikomo inu. Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano ku mawu a pemphero. Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikudabwa ndi angati akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero, mungolola izo zidziwike ndi inu pokweza dzanja lanu.

2 Atate athu Akumwamba, ife modzichepetsa tikubwera kwa Inu, Ambuye, kudzavomereza kuti ife sitiri oyenera kubwera. Koma chifukwa chakuti Yesu watipangira ife njira ndipo walipira mtengo wake, chotero, ife tikhoza kubwera molimba mtima ku Mpandowachifumu wa chisomo, mu nthawi ya kusowa. Ndipo tsopano, Ambuye, pamene ife tiri pano kuti tidzapereke Uthenga, chuma chofufuzidwa cha Khristu, ife tikukusowani Inu, Ambuye.

3 Ndipo pakhoza kukhala mmodzi wakhala pano, Atate, yemwe Inu mukuyesera kumuphunzitsa mwa njira yopambana, kuti Inu mukhoze kuwatumiza iwo kwinakwake, ku ntchito yaikulu imene Inu mwailinga. Ine ndikupemphera, Atate, kuti ngati izo ziri chomwecho, kuti usiku uno, kuti, cholinga Chanu chikwaniritsidwe. Ndipo tithandizeni ife pamene ife tikudzipereka tokha kwa Inu kwa utumiki.

4 Tsopano, Inu munawona manja onse, ndipo mukuyang'anabe pa iwo amene akwezedwa. Inu mukudziwa chimene chiri chosowekera. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izo, Atate. Ine ndikupereka pemphero langa limodzi ndi pemphero lawo, ndi zokhumba zawo ndi zokhumba zanga, pa Guwa lagolide pamene nsembe yathu ilipo usikuuno. Mu Dzina la Ambuye Yesu, ife tikupemphera kuti Inu munyeme Mkate wa Moyo, kwa ife, kuchokera mu Mawu Anu. Ameni.

Inu mukhoza kukhala pansi.

5 Ine ndikupepesa kuti ndachedwerapo pang'ono, kungoti ine ndamva kuti usikuuno izo zinali basi—mochedwerapo pang'ono, msonkhano unali kuyenda mochedwerapo pang'ono. Ndipo ife tidzazikonza izo, ndi kutulukamo mofulumira momwe tingathere. Tsopano ife tikufuna kuti tiyandikire Mawu, usikuuno, ndipo ndi zonse zomwe zinali mwa ife.

6 Ine ndikudziwa inu muli pano, inu, ena a oyimba abwino awa ine . . . Mel Johnson, kwa mmodzi, yemwe ine ndikumudziwa wakhala pano. Ine ndamupempha iye kuti atiyimbire, ife, nyimbo ija imene ine ndimalephera basi kuti ndiyichotse mmalingaliro anga. Nthawizonse ine ndimaing'ung'uza iyo, ya, "misonzi ikutsikira pansi." Ine—ine ndimaikonda imeneyo. Ndipo ine ndikuganiza iye adzayimba pa kadzutsa wa Amuna Amalonda, kapena kwinakwake, kwa ife.

7 Jim, ine ndikufuna kuti iwe ukhale wotsimikiza kuti undipezera ine imeneyo. Ndipo ngati iwe uli ndi tepi yaing'ono, undiyikire ine imeneyo, yapadera, chifukwa ana anga akufuna ayimvetsere iyo. Pamene ine ndakhala ngati ndatsika pang'ono, ine—ine—ine ndikamvetsera iyo, iyo imandipangitsa ine kumverera bwino, kumvetsera kuyimba kwabwino. Ndipo, Billy, ine ndikapita mu ofesi kumusi uko, ndipo iye amakhala nawo nthawizonse matepi amenewo anyimbo akuyimba nthawi zonse, ndipo ine ndikuganiza izo zimamuthandizira iye.

8 Inu mukudziwa, pali chinachake chokhudza nyimbo, chomwe chimakhala ndi mphamvu mwa iyo. Ife tonse tikudziwa zimenezo. Ife tiri—ife tikuzidziwa zimenezo. Mukuona? Ndizo, tayang'anani pa ankhondo, pamene iwo akuyimba nyimbo ndi kuimba zing'wenyeng'wenye. Kodi inu mumadziwa mafikiridwe a ku nkhondo, mu gulu la ankhondo a Mulungu, choyamba ndi nyimbo? Oyimba ankatsogolera likasa, akukondwera ndi kumayimba; kenako pamabwera likasa; ndipo zikatero nkhondoyo. Uko nkulondola. Chotero, amenewo ndiwo mafikidwe oyenera.

9 Ndipo ndi chifukwa chake timabwera mu msonkhano usiku. Kodi ife timachita chiyani? Kuimba nyimbo za Ambuye; ndipo kenako Likasa, Mawu, kuwerenga Mawu; ndipo kenako nkhondo, ndiye ndife—ife tiri mkati. Kotero mbendera zazikulu zikuwuluka, usikuuno; Dzina la Yesu Khristu, Ambuye Mulungu akhoza kukwezedwa, mdani nkuthamangitsidwa.

10 Ndipo, Mulungu, apambana chigonjetso usikuuno, ndipo apulumutsa miyoyo, achiritsa odwala ndi osautsika; apangitsa zimenezo, iwo amene ali ofowoka ndi otsika pansi, kuti adzutse mitu yawo ndi kusangalala, kudzitengera ulemelero waukulu kwa Iyemwini. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Ambuye Yesu.

11 Ine ndikufuna inu mutsegule, usikuuno, ndi ine, ngati inu muli nalo Baibulo lanu, ndipo nthawizina anthu amangolemba mutu waung'ono umene atumiki akuyankhulapo. Zinkachitika kuti ine ndimatha kuganiza za izi mofulumira ndithu, popanda ngakhale kuzilemba izo. Koma nditangodutsa kumene twente-faivi, bwanji, miyezi ingapo yapitayo, Ine ndikutanthauza nthawi yachiwiri, ndipo chotero izo zimapangitsa izo kukhala zovuta pang'ono kwa ine kuti ndizikumbukira. Ine ndiri ndi zipsyera zambiri kuchokera ku nkhondo. Ndipo pamene ife tikukalamba, ife sitimaganiza basi monga ife tinkachitira, ndipo ine ndiri. . .Pamene ine ndiyang'ana pa Lemba ndi kuwona, ndiye ine ndimakumbukira chimene mutuwo uli.

12 Tiyeni titembenuzire ku Yoswa, mutu wa 10, tiyambe kuwerenga pa ndime ya 12.

*Ndiye anayankhula Yoswa kwa* A*MBUYE* *mu tsiku pamene* A*MBUYE* *anawapereka a Amori pamaso pa ana*

> *a Israeli, ndipo iye anati pamaso pa Israeli, Dzuwa, yima iwe njii* pa *Gibeoni; ndipo*. . .*Mwezi,* pa *chigwa cha Ajaloni.*
>
> *Ndipo dzuwa linaima njii, ndipo mwezi unakhazikika, mpaka anthu anali atadzibwezera okha pa adani awo. Kodi izi sizinalembedwe mu bukhu la Yaseri? Kotero dzuwa linaima njii pakati pa thambo, ndipo silinafulumire kulowa pafupi tsiku lathunthu.*
>
> *Ndipo panalibe tsiku lotero nkale kapena pambuyo pake, kuti* AMBUYE *anamvera mawu a munthu: pakuti* AMBUYE *anamenyera Israeli.*

13 Ambuye awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake. Ine ndikufuna kuti nditenge mutu pamenepo kwa pafupifupi maminiti sarte, ngati ine ndingakhoze kuwugwira iwo kwa iwo: Chododometsa. Kungogwiritsa ntchito liwu limodzilo: *Chododometsa*.

14 Tsopano molingana ndi Webster, *chododometsa* ndi "chinachake chomwe chikuwoneka chodabwitsa, koma ndi choona," chotero chododometsa ndiye chingakhale chimodzimodzi monga chozizwitsa. Chododometsa ndi pamene chinachake chimene—chimene chikuwoneka ngati sichingakhoze kukhala, a—chidziwitso cha malingaliro aumunthu; zonse pamodzi ndizododometsa, komabe zatsimikiziridwa kukhala zoona. Tsopano, chozizwitsa chingakhale chinthu chomwecho, pakuti chozizwitsa sichingakhoze kufotokozedwa. Chozizwitsa ndi chinachake chimene chimachitika, ndipo iwe sungakhoze kuchifotokoza icho, chomwe chimachipangitsa icho kukhala chododometsa. Ndi chododometsa, komabe icho ndi choonadi.

15 Tsopano, anthu lero, ambiri amakono, amakhulupirira kuti masiku a zozizwitsa anapita. Iwo sakhulupirira kuti pali chinthu chonga cho—chozizwitsa. Koma, komabe, ine ndimakhulupirira kuti dziko ladzaza ndi zozizwitsa. Ine ndikukhulupirira kuti chododometsa chikumakhalapo mowirikiza.

16 Mwachitsanzo, ine ndimakhulupirira kuti membala aliyense wobadwanso mwatsopano wa Thupi la Khristu ndi chododometsa mwa iwoeni. Ine ndikukhulupirira aliyense wa inu Amethodisti ndi Apresbateria ndi Achilutera, amene sanalandirepo ubatizo wa Mzimu Woyera, munali mu mpingo wina wokhazikika umene sunkakhulupirira mu Kubadwa kwatsopano kwenikweni, ndipo tsopano munalandira ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi chitsanzo changwiro cha chododometsa. Chifukwa, chinachake chinachitika kwa inu, chimene chinasintha umunthu wanu wonse, ndipo aliyense akhoza kuyang'ana pa izo ndi kudziwa chomwe chododometsa chiri: chozizwitsa.

17 Pokhapokha izo zitachitika, inu simungakhoze kukhala Mkhristu. Payenera kukhala chododometsa, kuti inu mukhale Mkhristu. Chifukwa, palibe amene angakhoze—angakhoze kusintha mzimu mwa munthu, ndi kumupatsa iye Kubadwa kwatsopano, kunja kwa Mulungu. Mulungu yekha ndi Mmodzi yekhayo angakhoze kuchita zimenezo. Ndipo ndi chozizwitsa momwe Mulungu angakhoze kutengera kuganiza kwa munthu, ndi njira zake, ndi moyo wake, ndi chirichonse, ndi kuchisintha icho kuchokera ku chimene icho chinali, kupita ku chimene icho chingakhoze kukhala, chimene Iye angakhoze kuchipanga icho.

18 Mwachitsanzo, masiku angapo apitawo, ine ndinaitanidwa pa cho—chochitika, kapena pa chi—chinachake chaching'ono chikuchitika. Panali mnyamata wabwino, mnyamata wabwino kwambiri, iye ankayenda ndi mtsikana wamng'ono, mtsikana wabwino kwambiri wochokera ku banja labwino. Ndipo mnyamata uyu, mwadzidzidzi, anabwera ndi lingaliro linalake, ndipo iye anangochokapo. Iye anachita chinachake cholakwika kwa mtsikana wamng'onoyo, ndipo monga momwe anamulonjeza iye kuti adzachita chinthu chinachake ndiyeno iye sanachichite icho. Ndipo m'malo mobwera kwa mtsikanayo ndikudzapepesa, monga—njonda iyenera kuchitira, iye, izo sizinali basi mwa iye kuti achite zimenezo.

19 Ndipo abambo ndi amayi anandiyitana ine pa chochitikacho, ndipo anati, "Ife tikufuna kudziwa chimene chalakwika ndi mnyamata wathu."

20 Tsopano, sikophweka kuchita nthawizina, koma iwe uyenera kukhala woona ndi woona mtima. Chotero, mnyamatayo anali Mkhristu, ponena za wokhulupirira. Iye anali atalapa ndipo anali atabatizidwa, ndipo anali ndi udindo wake pakati pa okhulupirira, komabe anali asanalandire ubatizo wa Mzimu Woyera, ziribe kanthu momwe iye ankaganizira kuti iye anali nawo.

21 Iwe kumaganiza kuti uli nawo, ndi kukhala nawo Iwo, ndi zinthu ziwiri zosiyana. Iwe ukhoza kuyesera kunena kuti uli nawo, ndipo ukhoza kuwonetsa umboni wa kutengeka kwina; koma kupatula ngati moyo wako utamatsimikizira zomwe ukudzinenera kuti uli nazozo, iwe udakalibe Iwo. Ziribe kanthu kuchuluka kwa kutengeka, momwe iwe ungalumphire, kuthamanga, zomverera, kuyankhula mmalirime, kapena kufuula, kapena chirichonse chimene ungakhoze kuchiyikapo icho; zomwe ziri zabwino, ine ndimakhulupirira mu izo zonse, inenso; koma kupatula ngati moyo wako ukugwirizana ndi umboni wako, ndiye ulibe Iwo. Chifukwa, chipatso cha Mzimu chimatsimikizira chomwe iwe uli, chimodzimodzi monga ngati chipatso cha mtengo uliwonse chimanenera chimene icho chiri. Yesu anati, "Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo."

22 Tsopano, makolo a mnyamata uyu. Amayi ake ndi achi

German. Sikuti ndi kulimbana ndi German, koma muli chofooka m'banja limenelo. Ndipo, ndiko kuti, iwo amangokhala, ndipo iwe ukhoza kumayankhula nawo iwo, ndipo akhoza kumangokuyang'ana iwe pa nkhope. Iwo ali nazo... Mlongo wa mtsikana uyu, mayi wa mnyamata uyu, mlongo wake. Ine ndabwerapo ndikuyenda mu msewu, m'mawa wochuluka, ndipo dona wamng'ono uyu atakhala pabwalo, ndipo ine nkuti, "Mmawa wabwino, kwa inu." Iye amakhoza kungoyang'ana pa ine. Ndipo ine ndimakhoza kuyima, ndipo ndikudzanena kuti, "Mmawa wabwino ndithudi." Iye basi amangoimirira, nkumayang'ana kumene pa iwe; mkazi wanzeru. Ndipo ine nkudzati, "Udzabwere kudzatiwona ife nthawiyina." Iye amangoima ndi kumayang'ana. Chabwino, azichimwene ake amachita mwanjira imeneyo, abambo ake ndi amake ndi a choncho.

23 Tsopano bambo ake a mnyamatayo, ndi achi Irish mosamalitsa, wolunda, ndipo osachedwa-kunyanyuka, osachedwa kupsya-mtima. Ndizo banja lake lonse ndi choncho, kupatula ngati wina kuchokera m'banjalo, atembenuzidwa. Tsopano mu izi, mnyamata uyu...

24 Bambo ndi amayi awa, onse ndi Akhristu, odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo amulera mnyamata uyu mu njira ya Ambuye. Ndipo tsopano mnyamatayo ali pafupifupi usinkhu wa zaka seventini kapena eyitini, chinachake pamenepo, mwana wabwino kwambiri, ndipo iye—iye wakhala mnyamata wachitsanzo weniweni kunyumba, mwana wabwino. Ndipo ali ndi mchimwene wake yemwe ali mosinthanitsa basi.

25 Koma atsikanawo, banja la amayi, amakhala pafupi ndi... tchalitchi chabwino. Koma kodi inu mukuganiza kuti iwo angabwere konse kumeneko? Ayi. Ndipo iwo amadziwa kuti Izo ndi zolondola, koma izo siziri mwa iwo basi—kupempha chikhululukiro kapena kupempha kukhululukidwa. Iwo basi sangachite zimenezo. Izo siziri basi mwa iwo.

26 Tsopano majini mwa abambo ndi amayi a mnyamata uyu, ziribe kanthu kuti iwo atembenuzidwa mochuluka bwanji, akadali mnofu womwe unalumikizidwa kwa mnyamata uyu. Chotero, mwanayo ali ndi kuipidwa mwa iye, chimodzimodzi basi monga zochokera ku banja la amayi ake, ndipo iwo samakhululuka, iwo sangapepese, ndipo ndi pamene mnyamata ameneyo wayima.

27 Tsopano, ine ndinanena kwa abambowo, "Ziribe kanthu kuti inu mwamulera chotani iye..." Ine ndinati, "Tsopano tayang'anani pa inu, kuchokera ku banja lanu: onse a iwo, oledzera, ndi—ndi omenyana, ndi owomberana, ndi odulana, ndi zina zotero."

28 "Tsopano tayang'anani pa banja lanu," kwa amayi. "Iwo ndi gulu la anthu, amangokhala pamenepo ndipo osayankhula,

odziyimira pawokha, ndi zina zotero, osalemekeza chipembedzo. Koma," Ine ndinati, "si iweyo. Ndiwe mmodzi yekha mwa alongo ako ndi abale, ndipo ndiwe wokoma, wachifundo, ndi wokhululuka. Nchiyani chimachita zimenezo? Ndipo ndiwe mtengo, gawo la mtengo wa banja umenewo, komabe unalandira Mzimu Woyera. Ndicho chinthu chimene chinakupangitsa iwe kukhala wofewa ndi wokoma. Si anthu ako panonso, ndi Khristu wako amene amakhala mwa iwe."

29 Ine ndinati kwa mnyamatayo, "Tayang'ana pa banja lako, pafupifupi onse a iwo ndi zidakhwa, ndi zina zotero." Ine ndinati, "Ndipo olunda bwanji, ndi—ndi okupsya-mtima, ndi osachedwa-kukwiya, koma iwe sichoncho. Ndiwe wachifundo, wokhululuka. Ndi chiyani chimenecho? Mzimu Woyera. Iwe sindiwenso chimene iwe uli; ndi Khristu mwa iwe." Ine ndinati, "Tsopano chinthu chomwe chomwecho chiyenera kuchitika kwa mwana wako."

30 Ndipo abambo anadzuka ndipo anati, "Mwana wanga anapita ku guwa. Iye anabatizidwa molondola, mu Dzina la Yesu Khristu, ndi ubatizo wa madzi mu dziwe." Anati, "Ine ndikudziwa mwana wanga wabwera kwa Khristu."

31 Ine ndinati, "Izo zikhoza kukhala zabwino, machitidwe onse akunja. Iye akhoza kuzindikirika ngati wokhulupirira limodzi ndi okhulupirira. Koma mpaka iye atasinthidwa, atabadwanso mwatsopano, ine ndingamulangize mnyamata ameneyo kuti asadzamukwatire konse mkaziyo. Iye adzapanga Gehena pa dziko lapansi kwa iye, mpaka mzimu wodekha, wokoma, wokhululuka wa Khristu utadzalowamo. Ndiye icho chidzakhala chododometsa mwa icho chokha, kutenga chikhalidwe chomwe cha mnyamata yemwe analeredwa pakati pa abambo ndi amayi. Ndipo komabe, mu luntha lake, iye akuyesetsa mwakukhoza kwake kuti agonjetse izo. Iye sangakhoze kuchita zimenezo. Iye sadzachigonjetsa konse icho. Khristu adzayenera kuti adzachigonjetse icho. Pamene iye amulola Khristu kulowa, akatero iye wagonjetsa kale pamenepo. Icho chidzakhala chododometsa changwiro, pamene munthu abadwa mwa Mzimu wa Mulungu.

32 Ine ndawonapo otsutsa akuimirira ndi kuseka, ndi kumapitirira, za chitsitsimutso cha Mzimu Woyera. Ndipo patapita kanthawi, Mulungu amamugwira munthu yemweyo ndi kumusintha iye, ndipo apa iye wayima pa guwa akulalikira chinthu chomwecho chimene iye ankadana nacho kamodzi. Ndi chododometsa, momwe kuti Mulungu angakhoze kumutengera wosakhulupirira ndi kupanga wokhulupirira mwa iye.

33 Tsopano ine ndikudabwa, ngati munthu amaganiza kuti zozizwitsa zinapita, ine ndikudabwa kuti ndi mtundu wanji wamankhwala asayansi omwe ungamupatse munthu woteroyo kuti asinthe malingaliro amenewo mwa iwo, kuti achotse

udani ndi njiru ndi ndewu, kuzitulutsamo? Palibe mmodzi amene angakhoze kuzifotokoza izo. Koma ndi chododometsa, chifukwa ndi chozizwitsa cha Mulungu. Pamene munthu asinthidwa kuchoka ku umunthu umene iye ali, kukhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu, iye amadzakhala chorengedwa chatsopano. Iye samakhalanso chimene iye anali. Iye amadzakhala mwamtheradi cholengedwa chatsopano mwa Khristu.

34 Dziko ili palokha, limene ife tikukhalamo, ndi chododometsa mwamtheradi, momwe ilo linapangidwira. Ife tikupeza kuti, mu Ahebri mutu wa 11 ndi ndime ya 3, kuti, "Dziko linakutiridwa pamodzi ndi Mawu a Mulungu." Kodi Mulungu anazitenga kuti zipangizo zopangira dziko lapansi? Kodi Iye anachita motani izo? Baibulo limanena kuti ilo "linapangidwa ndi kukutiridwa limodzi." Mapangidwe ake onse ndi gawo lake anaikidwa pamodzi ndi Mawu a Mulungu. Ngati icho si chododometsa, ine sindikudziwa kumene icho chiri. Ndi kuti kumene ife tikanakhoza kupanga ndi kunena kuti Iye anapeza zipangizo, pamene kunalibe zipangizo? Iye ankayenera kuti aliyankhule ilo mu kukhalapo. Ndi chododometsa, kuti dziko lino liri pano usikuuno.

35 Chinthu china, ndi chododometsa cha momwe ilo limakhalira mu kanjira kake, likulendewera mumlengalenga. Ilo lingakhoze bwanji kulendewera apo mmalo amodzi awo, kumazungulira monga *chonchi*, pafupifupi mailosi leveni handiredi pa ora? Mailosi twente-foro kapena twente-faivi kumazungulira, ndipo kumapita mozungulira maora twente-foro aliwonse, mwangwiro kwambiri mwakuti ilo silimaphonya sekondi imodzi. Kutembenuka kwangwiro, bwinoko kuposa pafupifupi a . . . Kuposa mailosi sauzande pa ora, limatembenuka mozungulira monga *chonchi*, likulendewera mu mlengalenga. Ngati ilo litati likwere mmwamba kapena pansi, mulimonse, bwanji, mai, ilo linga—ilo lingasokoneze dongosolo lonse la dongosolo la Mulungu la kayendedwe ka dzuwa. Ndipo ilo limapita kukazungulira equator, kuzungulira kanjira kochuluka kwambiri, nthawi ya chaka, izo sizimalephera konse, nyengo ndendende basi.

36 Ndiwuzeni ine chimene chimaligwira ilo kumwambako, chimene chimalitembenuza ilo mwaangwiro kwambiri mu nthawi. Inu mukhoza kupeza wotchi; ine sindikudziwa kuti mungalipire ndalama zingati pa imodzi, madola sauzande; ndipo wotchiyo, mkati mwa mwezi umodzi, idzataya maminisi. Iwo alibe chirichonse chimene chingagwire ntchito mwangwiro, komabe dziko lino limatembenuka mwangwiro. Chifukwa chiyani? Ndi Mulungu akuchita zimenezo. Ndi chododometsa. Mulungu analilamulira ilo kuti lizichita zimenezo, ndipo ilo limachita zimenezo.

37 Nanga bwanji mwezi? Komabe mamillioni a mailosi

kutalikirana ndi dziko lapansi, ndipo komabe iwo—iwo umalamulira mafunde pa dziko lapansi. Mamillioni a mamailosi kutalika, chikoka chake, choyima mu danga lake. Kumaima mu kanjira kake, ilo limakopa dziko lapansi. Pulaneti iliyonse imakopa imzake, pokhala pamalo ake.

38 Oh, ulaliki wotani umene ine ndingakhoze kuwutenga kuchokera pano, phunziro! Momwe kuti cholengedwa chirichonse cha Mulungu chitakhala m'malo mwake, icho chingakope chimzake. Koma ife timathamangira pa kunyanyuka kwina kolusa kwinakwake, ndi kukapanga bungwe ndi kudzilekanitsa tokha, mowoneka osamakhala nacho chikhulupiriro, ndiyeno ife tiri nalo dongosolo lonse la Chikhristu litasokonezeka. Ngati munthu aliyense akanakhala mmalo ake, icho chikanakhala chododometsa cha Mulungu, kuwona momwe Mulungu angawabweretsere Achipresbateria, Achilutera, Abaptisti, Amethodisti, Akatolika, ndi onse pamodzi. Ngati tingabwerere ku Mawu a Mulungu, icho chingakhale chododometsa chenicheni. Ndiyeno mpingo wonse ukhoza kugwirizana, osati pa tizikhulupiriro tanu ndi zina zotero, koma pa Mawu, momwe Iwo analembedwera. Chifukwa, "Iwo alibe kutanthauzira kwamseri," limatero Lemba.

39 Momwe kuti mwezi umenewo umalikopera dziko lapansi! Kuno osati kale kwambiri, mzanga wa ine, woyandikana naye wanga, anali kukumba maenje a zitsime zamafuta, kumusi mu boma la Kentucky. Ndipo pamene mwezi umenewo uyamba kumatulukira kumeneko, mafunde amenewo amabwera njira yonse kudutsa pa dziko lapansi. Madzi amchere amenewo, pansi mdzenje limene iwo anabowola, amakwera mmwamba pamene mwezi umenewo ukubwera. Ziribe kanthu, ngati iwo ali pansi mapazi handiredi pansi . . . kapena pamwamba pa dziko lapansi pano. Amapita pansi mahandiredi a mapazi, komabe, pamene mwezi umenewo ukutembenuka, madzi amenewo amakwera kuti akakomane nawo iwo. Izo zinatero.

40 Inu simungakhoze kubisa chirichonse, pamene Mulungu walamula izo. Izo ziyenera kumumvera Mulungu, pamene Mulungu apereka lamulo Lake. Ndi chifukwa ine ndikudziwa kuti Iye adzakhala nawo "Mpingo wopanda banga kapena khwinya," Mulungu analamula izo chomwecho. Iwo uyenera kumvera. Mulungu adzakhala nazo izo, chifukwa Mawu a Mulungu anena chomwecho.

41 Momwe mafunde, mwezi, ndi chirichonse, zimakopa zochitika za padziko lapansi! Inu mutenge . . .

42 Ife timawona nyenyezi ikuwombera, ife timaitcha iyo nyenyezi, imeneyo si nyenyezi yowombera, iko ndi kuwala, ndithudi ife tikuzidziwa zimenezo, koma ife timaitcha iyo nyenyezi. Nyenyezi imeneyo siyingakwanitse kusuntha mpaka kutali chomwecho. Ngati nyenyezi imodzi itachoka mu kanjira

kake, iyo mwinamwake ingakope chirichonse mu mkombero, mu chirengedwe chonse, iyo ingatero—iyo ingasokoneze. Chirichonse chiyenera kukhala mu malo ake, kuti zikasunge dongosolo la Mulungu kumayenda.

43 Chotero ife tiyenera kumakhala mmalo athu, ife tiyenera kumakhala ngati ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ngati ife tikanati tisagwe konse kumbuyo uko, chinthucho chikanakhala chikutembenuka, sipakanakhala imfa kapena china chirichonse. Koma mathokozo akhale kwa Mulungu, pakubwera chododometsa, pamene Mulungu Mwiniwake adzamukhazikanso iye pamalo pamene iye ayenera kukhalapo. Inde, chododometsa.

44 Munthu amene samakhulupirira mu—mu chododometsa, ndipo samakhulupirira mu zozizwitsa, inu mungalungamitse bwanji luntha lanu, ndi kumayang'ana mmaso a zinthu zimene inu simungakhoze kuzifotokoza? Ndi zosatheka kwathunthu kuti munthu aliyense afotokoze mmene dziko lingaziyendetsere lokha ndi kukhala mu nthawi yangwiro, ndipo (nthawizonse) dongosolo lonse la dzuwa ndi zinthu zimenezo, ndipo momwe mwezi ungalikopere dziko lapansi. Ndipo ndi zinthu zina zingati zimene ife tikanakhoza kuzikamba!

45 Momwe—utomoni mu kugwa kwa chaka umapita pansi ku muzu wa mtengo, popanda luntha lirilonse kuti likayendetse izo kumeneko, kubweretsedwanso mu kuphukira kwa chaka, ndi moyo watsopano, bwanji, ndi chododometsa. Palibe amene angakhoze kuzifotokoza izo. Ife sitimadziwa momwe izo zimachitikira. Koma Mulungu amachita zimenezo, chotero ndi chododometsa, mosalekeza. Ndi chinsinsi momwe Mulungu amachitira izo. Ife timayang'ana pa izo mochuluka kwambiri mpaka izo zimakhala zofanana kwambiri, ife timayang'ana pamwamba pa izo.

46 Ndipo ndiro lomwe liri vuto ndi (ife) anthu Achipentekoste. Ife tamuwona Mulungu akuchita zododometsa zambiri mpaka izo zangokhala mwa apo ndi apo kuti ife timaziganizira izo nkomwe. Ngati titangoima miniti ndi kulingalira! Mulungu ali konsekonse. Mulungu ali—akuchita. Ndipo chowonera nthawi Yake chakale chikugunda mozungulira, mpaka potsiriza icho chidzapita mpaka ku Umuyaya, chifukwa Mulungu walonjeza izo kudzachita zimenezo. Tsopano ife tikudziwa kuti chiripo chododometsa.

47 Tsopano, mmbuyo mmasiku a Nowa, mvula isanabwere, ndi chigumula, chinali ndithu—chinthu chovuta kwa Nowa, mu m'badwo wawukulu waluntha uwo umene iye anakhalamo, kuyesetsa kuwauza anthu, mwa Mawu a Mulungu, kuti ikudzavumba mvula. Tsopano, izo zikanadzachitika, mosakayika, kuti izo sizinafikire pa—kuyenerera kwa kafukufuku wawo wa sayansi, munalibe mvula mu mlengalenga.

Koma, inu mukuona, Nowa anati kudzakhala mvula chifukwa kuti Mulungu anati kudzakhala mvula. Ndipo Nowa, mwa chikhulupiriro, mvula isanabwere nkomwe, iye anati iyo idzakhala pamenepo.

48 Ndi chifukwa chake ife tikunena chinthu chomwecho. Kuti, iwo amati, "Bwanji, Yesu, iwo anati Iye anali kubwera nthawi yayitali kale. Mahandiredi a zaka zapitazo, iwo ankadzinenera kuti Iye anali kubwera. Atumwi ankanena chomwecho; mwina m'badwo wawo." Izo sizimaimitsa izo mpang'ono pomwe. Ife tikudziwabe kuti Iye akubwera. Kodi izo zidzakhala motani? Ine sindikudziwa. Koma Mulungu adzamutumiza Iye. Iye analonjeza kudzatero, ndipo ine ndikudziwa Iye adzakhala pano.

49 Tsopano, Nowa akanangonena kuti, "Mulungu wanena chomwecho." Koma, inu mukuona, ndiye, pambuyo pa zonsezo, izo sizinakwaniritse chivomerezo chawo cha sayansi mu tsiku limenelo. Koma pamene nthawi inadzafika yoti Mawu akwaniritsidwe, iyo inavumba, mofanana basi. Icho chinali chododometsa ndithu mu tsiku limenelo, kuganiza kuti mvula ikhoza kubwera kuchokera kumwamba, kumene kulibeko mvula.

50 Koma ngati Mulungu atengedwa pa Mawu Ake, Iye akhoza kuchita, kupanga chododometsa. Iye akhoza kuchita chozizwitsa. Ndipo munthu aliyense yemwe wabadwa mwa Mzimu womwewo umene umachita zozizwitsa, bwanji, ndi chinthu chophweka kuti iye akhulupirire zozizwitsa, chifukwa iye ndi gawo la Mulungu. Ameni.

51 Mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu; osati mwa chipembedzo, osati mwa kachikhulupiriro, osati mwa kugwirana chanza; koma mwa kubadwa, kuti inu munafa ku luntha lanu lomwe, ndipo munabadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Ndipo ndinu chododometsa, inueni, momwe kuti inu mwasinthidwa kuchoka ku imfa mwapita ku Moyo. Kuchokera mkati mwanu mwenimweni muli cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu. Ndicho chododometsa.

52 Mulungu amayankhula Mawu Ake, ana Ake amawakhulupirira Iwo ndi Mulungu. Sayansi siyingakhoze kutsimikizira momwe izo zingakhoze kuchitikira; iwo sakudziwa kanthu za zimenezo. Koma ana amakhulupirira izo, mulimonse, ndiyeno Mulungu amachita chododometsa, amazipangitsa izo chomwecho. Amazipangitsa izo chomwecho, chifukwa Mawu Ake amene anayankhula dziko nkukhalapo, akhoza kubweretsa, akhoza kupangitsa mawu aliwonse, omwe Iye anayamba wawalonjeza, kufika podzachitika.

53 Ndi chifukwa chake Abrahamu sanadzandime pa lonjezo la Mulungu, kudzera mu kusakhulupirira, koma anali wokhutitsidwa kwathunthu kuti Iye anali wokhoza kuchita ndi kusunga chimene Iye anati Iye akanadzachita. Iye sanadzandime

pa lonjezo la Mulungu, pokhala usinkhu wa zaka handiredi, ndipo Sarah nainte, kuti akhale naye mwana uyu. Chifukwa chakuti iye ankadziwa kuti Mulungu akanakhoza kuzichita ndi (kupanga) kukhala ndi chododometsa kuti chichitike pa chinachake, chozizwitsa kuti chichitike, ndipo Iye anachichita icho.

54 Ana Achihebri. Tsopano kodi inu mungaipangitse bwanji sayansi kukhulupirira lero kuti munthu akhoza kupita mu ng'anjo? Oh, ine ndikhoza kuchita mantha kunena kuti ndi ma Fahrenheit angati momwe unatenthera; koma anakhoza kupita mu ng'anjo imeneyo kumbuyo uko, mu Bukhu la—la Danieli, ndi kukhala mu ng'anjo imeneyo mpaka iwo ankaganiza kuti iye, iwo anali onse atawotchedwa mpaka phulusa. Chimene, ngakhale amuna, ankhondo aakulu a asilikari, amuna akhungu aakulu amene anasunthira kumeneko kuti—kuti awaponyere iwo mu ng'anjoyo, amuna amenewo amene analowa mmenemo anafa, ndi kutentha kwakukulu kwa ng'anjo yoyatsira iwo. Ndipo iwo anagwera mu ng'anjo, ndipo anali pansi mmenemo kwa nthawi yonse iyi, ndipo anatulukako opanda ngakhale fungo la moto pa iwo.

55 Mulungu, akuchita chozizwitsa! Chimenecho chinali chododometsa chenicheni, chosunga mphamvu ya Mulungu, motsutsa mdani aliyense, pamene munthu ali wokonzeka kuvomereza kuti Mulungu ndi woona. Ndipo Mulungu amasunga Mawu Ake ndi kuwalemekeza iwo amene akhulupirira mwa Iye. Ndithudi ine ndimakhulupirira mu chododometsa.

56 Yoswa, wankhondo wamkulu yemwe ine ndangomuwerenga kumene, mphindi zingapo zapitazo, mu Bukhu la Yoswa, mutu wa 10. Zindikirani, Yoswa anali a—bwenzi la Mulungu. Iye anali msilikali, a—kazembe, ndipo iye anabwerapo pansi pa kukopa kwa mneneri, Mose. Ndipo Mose anali atatengedwa, ndipo Yoswa analamulidwa kuti awatenge ana kukalowa mdziko lolonjezedwa, ndi kukagawa malowo. Kusamvera kwa ana; ndipo Mose anali atayembekezera kuti akalambe, ndipo kotero Yoswa anabwera kuti adzatenge malo a Mose, kuti adzakhale mtsogoleri wankhondo wa Mulungu.

57 Ndipo Yehova anayankhula kwa iye, ndipo anati, "Monga ine ndinali ndi Mose, momwemonso Ine ndidzakhala ndi iwe." Izo ndi zabwino mokwanira kwa Joshua. Anati, "Khalani wamphamvu, ndi wolimbika mtima ndithu, pakuti Ambuye Mulungu wako ali ndi iwe kulikonse kumene iwe upita. Ndipo malo aliwonse amene zidendene za mapazi ako zidzapondapo, amenewo Ine ndakupatsa iwe." Ndiye, mphondero zimatanthauza kukhala nacho. Dziko lonse linali lawo. Ilo linali lonjezo.

58 Kale izo zisanachitike nkomwe, pamene iye anabwera

kumusi uko ndi Kalebu ndi azondi ena, ndipo iwo anawona kutsutsa kwakukulu, Amaleki, ndi—ndi Aperezi, ndi Ahiti, ndi ena otero, onse atatchingidwira mkati, ndipo kumeneko ku Yeriko amakhoza kuchitirapo mjaha wa magaleta pamwamba pa—pa malopo, ndi munthu wopambana wazimphamvu. Mwakuti, ena a—osakhulupirira pakati pawo, anati, "Bwanji, ife tikuwoneka ngati ziwala pambali pa iwo."

59 Koma Kalebu anati, ndi Yoswa, "Ndife oposa kukwanitsa kulitenga ilo."

60 Chifukwa chiyani? Mulungu anati, "Ine ndakupasani inu dziko ili." Ziribe kanthu kuti kutsutsa kunali chiyani, kwakukulu bwanji ndi—ndi—ndi—zinkawoneka zovuta, komabe Mulungu anati linali lawo. Oh! Mulungu ndi wokhoza kusunga chimene Iye walonjeza.

61 Icho chinali chododometsa, kuwona anthu odzadza mdzanja, opanda zida, pafupifupi, koma zimene iwo anali atatola mchipululu, ndi kumene iwo anali atawathamangitsa amuna ena, mwinamwake ndi maleki akale ndi macheka, ndi chirichonse chimene iwo akanakhoza kuchigwira. Kukalowa mmenemo ndi kukawamenya amuna amenewo, amene anali zimphona. Icho chinali chododometsa. Mulungu ankadziwa kuti iwo anali nako kulimba mtima kuti akachita zimenezo. Ndipo Iye anawapatsa iwo lonjezo, ndipo anakalowa umo ndi kukachita ndendende chimene Mulungu anawalonjeza iwo kuti akachita.

62 Tsiku lina, mu kutentha kwa nkhondo, pamene mafumu anachita pangano lalikulu pakati pawo ndipo anatsikira kwa Yoswa ndi ana a Israeli. Kuti, Mulungu anali atawalonjeza iwo dzikolo. Ndipo iye anali atamugonjetsa mdani, ndipo iwo anali mu nkhalango ndi mapiri, atamwazikana kudutsa mchipululu kumeneko, ndipo Yoswa anayang'ana ndipo iye analiwona dzuwa likulowa. Iye anadziwa ngati magulu ankhondowo angapeze mwayi wodzilowetsa okha ndi—ndi kubwereranso kwa iye, bwanji, iye ankadziwa kuti iye akanadzakhala ndi kuvutika pawiri ndipo mwinamwake akanadzaluza amuna ambiri, ngati iwo angapeze konse malo oti adzilumikizize iwoeni limodzi.

63 Pamenepo ndi pamene, atumiki, pamenepo ndi pamene ife timalepherera. Apo ndi pamene mpingo umalepherera. Pamene chitsitsimutso ichi chimene ife tangokhala nacho kumene, misonkhano yayikulu iyi yomwe inayamba kudutsa dzikoli, pamene ife tinali ndi mdani akuthawa, ife tinkayenera kumusiya iye azithawa. Koma, chinthu chake ndi chakuti, ife timangokhalira kukwiya ndi zina zotero, ndi midadada yaikulu ya zinyumba ndi "kumapanga ochuluka akhale a magulu athu," ndi zina zotero. Ndipo apo inu mukumabwera, ndi kumadzilekanitsa tokha ku Mawu, ndi kutenga *izi*, *izo*, ndipo kenako nkumamanga enanso a mabungwe awo, ndi kuyambitsa

chinachakenso. Umo ndi momwe zimakhalira nthawizonse. Umo ndi momwe zinkakhalira mmasiku a Luther, Wesley, ndi Moody, Sankey, Finney, Knox, Calvin, njira yonse mpaka mmusi. Izo zakhala mwanjira yomweyo. Iwo amachotsa maso awo pa—pa chitsitsimutso, ndi kuchitengera icho pa zomwe iwo angakhoze kudzichitira okha.

64 Koma inu mukudziwa chimene chinachitika? Yoswa sanali munthu wa mtundu umenewo. Iye ankasowa nthawi. Dzuwa linali likukalowa, ndipo iye ankadziwa ngati mdani akanamanga konse . . . Chitsitsimutso chinali pafupifupi kumapeto kwa kutha kwa icho, monga ife tikuyimira lero. Iye ankadziwa kuti ngati iye akanati adikire konse mpaka mdani atamutchingira iye, izo zikanakhala zovuta kuti apambane nkhondo imeneyo. Inu mukudziwa chimene iye anachita? Iye ankadziwa kuti Mulungu analonjeza dziko limenelo. Iye ankasowa nthawi yochulukirapo. Kotero dzuwa litatsala pang'ono kulowa, ndiye iye anati, "Dzuwa, ima njii." Ameni. Chododometsa, ndithudi. Ndipo dzuwa limenelo linayima pamenepo kwa tsiku lathunthu, ndipo silinasunthe nkomwe; ndipo mwezi pa Ajaloni, sunasunthe nkomwe, nawonso.

65 Chifukwa, Baibulo linanena apa, kuti, "Inali isanakhalepo nthawi nkale, kapena kuyambira pamenepo, monga choncho, kuti Mulungu anamvera liwu la munthu."

Inu mukuti, "Oh, ngati ine ndikanadziwa ife tikanangokhala moyo mu tsiku limenelo!"

66 Yesu anati, mu Marko Woyera 11:24, "Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, 'Sunthidwa,' ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti zomwe inu mwanena zidzachitika, inu mukhoza kukhala nazo zimene inu mwanenazo." Chikadali chisomo, ndi chododometsa, mpaka mmusi mu m'badwo wathu. Ndithudi.

67 Mwezi ndi dzuwa limenelo zinaima mpaka Yoswa anamenyera njira yake kuti adutse, ndi Israeli, ndipo anadzibwezera okha chilango pa adani awo. Chifukwa chiyani? Izo zinali mu mzere wa ntchito.

68 Tsopano ngati inu mungapite kunja kuno ndi kukanena kuti, "Phiri, suntha! Ine ndikufuna ndikuwonetseni inu kuti ine ndikhoza kuchita zimenezo." Izo sizingachite zimenezo.

69 Koma ngati izo ziri mu mzere wa ntchito, pamene Mulungu wakulamulirani inu kuti muchite chinachake! Monga Iye ananena kwa Mose, "Chifukwa chiyani ukulirira kwa Ine? Yankhula kwa ana."

70 Anthu lero akukhalira kulira nthawi zonse, "Ambuye, ndi chiyani chotsatira, ndi chiyani chotsatira?" Ingoyankhulani ndipo kazipitani patsogolo! Uko nkulondola. Mulungu watituma ife kuti tikachite chinachake, tiyeni tikachichite icho. Musamaime pozungulira ndi kumaziganizira izo, kumati, "Kodi

izo zingachitike motani? Chabwino, *ichi* ndi icho." Zikupanga kusiyana kulikonse; ngati Mulungu anati chitani icho, chitani icho mulimonse. Iye akadali Mulungu wa zozizwitsa.

71 Yoswa, icho ndithudi chinali chododometsa pamene dzuwa ilo linaima nji. Ine ndinali kuyankhula ndi a—wasayansi ku sukulu nthawi ina, ndipo iye anali mphunzitsi wa Baibulo. Ndipo iye anati . . . Ine ndinalozera izi kwa iye. Ine ndinati, "Ine ndimaganiza inu mumanena kuti—dziko lapansi linatembenuka mozungulira, mwaona, ndipo—ndipo dzuwa linayima nji?" Ine ndinati, "Nanga bwanji Baibulo mwangotiuza kumene kuti linali loona? Mulungu . . . Yoswa anati, 'Dzuwa, ima nji.'" Chabwino, iye sakanakhoza kuyankha limenelo.

72 Koma dzuwa linaima nji. Izo sizinapange kusuntha kulikonse, inu mukuona. Ndizo kuti dziko lapansi linayima kwenikweni. Ndipo tsopano inu mukuti . . .

Iye anati, "Dziko lapansi linayima."

73 Ine ndinati, "Inu munati, 'Ngati dziko litaima, ilo lingataye mphamvu yake yokokera pansi ndipo aliyense angagwe kuchokera pamenepo.' Tsopano kodi inu muchita chiyani?"

74 Ndi chododometsa. Ameni. Mulungu anayimitsa dziko lapansi lonse kuti lisatembenuke, ameni, chifukwa munthu anati, "Ima nji pamenepo, mpaka ine ndimenye nkhondo iyi." Chimenecho ndi chododometsa. Ameni.

75 Icho chinali chododometsa pamene magulu ankhondo onse a Israeli anali atachirikizidwa pangodya, ndipo iwo anachita mantha ndi chimphona china chachikulu chonga cha mbiriyakale isanachitike chitayima pamenepo, dzina lake Goliati. Ndipo kumeneko ankhondo a Israeli, Sauli wophunzitsidwa bwino, mutu ndi mapewa pamwamba pa ankhondo ake onse, ndi kumagwedezeka mu nsapato zake. Palibe amene akanakhoza kulimbana ndi kubhetchera kwa munthu uyu wa tsiku limenelo.

76 Kunabwera kamwana kakang'ono, wosawoneka bwino, wamapewa akugwa, wolemera pafupifupi mapaundi nainte, wokhala ndi chidutswa cha chikopa cha nkhosa atazikuta momuzungulira iye monga choncho. Iye anati, "Manyazi pa ankhondo awa a Mulungu wamoyo; kuima pano ndi kulola Mfilisti wosadulidwa uyo azinyoza ankhondo a Mulungu wamoyo."

77 Pamene mawuwo anafika kwa Sauli, Sauli anati, "Sindiwe kanthu koma mnyamata, ndipo iye ndi wankhondo kuyambira ubwana wake. Ndipo ndiwe mwana, ndipo taona chimene iye ali. Bwanji, iwe sukanakhoza kupita momutsutsa iye."

78 Koma kodi iye anatenga chiyani? Iye sanatenge konse mkondo, iye sanatenge konse lupanga, koma iye anatenga legeni. Ndipo malo amodzi okha akanakhoza kugunda

chimphona chimenecho, amenewo anali pamphumi pomwe, pomwe zida zake zimagwera pankhope pake kuti ziwabise maso ake. Ndipo mwala uja, ndi mtunda wautali kuchokera pa mkondo wa singano wa mapazi fortini umene iye anali nawo mdzanja lake; zonsezo anali atazitulutsa bola ngati zinalipo, akanakhoza kumunyamulira nazo Davide wamng'ono ndi kuchita chirichonse kwa iye, ndi kumupachika iye mu mtengo, monga iye ankawopsyezera kuti atero, ndi kulola mbalame zidye mtembo wake.

79 Koma chinachitika ndi chiyani? Pamenepo panali chododometsa, pamene Mulungu anatenga kamwana kakang'ono kamunthu kosawoneka bwino nkomwe, mpang'ono pomwe, sikanali nkomwe msirikali wophunzitsidwa, mwana chabe yemwe anali ndi chikhulupiriro mwa Iye, ndipo anachititsa dziko lonselo manyazi. Mulungu anachita izo mwa chododometsa.

80 Ameni! Iye akadali Mulungu, usikuuno, wa chododometsa, mofanana basi monga Iye anachitira nthawi imeneyo.

81 Iye anapangitsa gulu lonse lankhondo kuchita chiwawa. Iwo anawona izo, ndipo anayamba kuthamanga ndi kumachokapo, chifukwa iwo anawona kuti mwa munthu wamng'onoyo munali chikhulupiriro mwa Mulungu Yemwe akanakhoza kusintha chirengedwe chonse, amachita chirichonse chimene Iye akufuna kuchita, pamene munthu akhulupirira Mawu Ake. Ndithudi. Ine ndikukhulupirira icho chinali chododometsa.

82 Mose, munthu wamkulu wankhondo yemwe anayesa kuwombola Israeli, ndipo sanathe kuchita zimenezo. Iye ankafuna kuwawononga Aigupto. Iye anamuwononga munthu mmodzi, ndipo iye analowa mu vuto chifukwa cha zimenezo, kuchita izo mwa chifuniro chake chomwe. Komano iye anatenga ndodo, ndodo yakale yowuma kuchokera ku chipululu, ndipo anapha nayo gulu lankhondo lonse. Ameni. Ngati chimenecho si chododometsa, ine sindikudziwa chifukwa chake. Pamene iye anakantha ndodo ija pa nyanja, ndipo naitanira kuti nyanja itseke; ndipo iye anamiza Igupto, fuko lonse, nthawi imodzi, ndi ndodo mdzanja lake. Ameni.

83 Icho chinali chododometsa, momwe iye anatsogolera Israeli kudutsa mchipululu, ndi kwa zaka forte. Ndipo pamene iwo anatuluka, apo panalibe munthu wofooka pakati pawo. Chimenecho ndi chododometsa. Inde, bwana. Iye anali munthu wamkulu bwanji, chimene Mulungu anamuchitira iye, chifukwa iye anakhulupirira Mulungu! Icho chinali chododometsa. Inde, bwana.

84 Icho chinali chododometsa, pamene Mulungu anasankha munthu mmodzi wamng'ono, dzina lake Mikaya, pamaso pa aneneri foro handiredi ophunzitsidwa bwino a Israeli, chifukwa

munthu uyu anali wololera kuti akhale ndi Mawu a Mulungu pamene otsutsa onse amamutsutsa iye.

85 Pamene foro handiredi anati, "Ah, kazipitani kumeneko!" Iye anati kwa Ahabu ndi Yehosafati, "Kazipitani kumeneko, Ambuye ali ndi inu. Ife tangopeza kumene vumbulutso. Ambuye ali ndi inu. Pitani uko, inu mukawakankhira iwo kutali kwenikweni kuwachotsa mdziko lathu, chifukwa ilo ndi lathu. Mulungu anapereka ilo kwa ife. Yoswa analigawa dzikolo, ndipo ili ndi lathu. Ndipo apo pali Afilisti kumtunda uko, akudya tirigu kuchokera m'minda yathu. Bwanji, sizikusowa kuganiza, vumbulutso lathu ndi lolondola."

86 Ndiye momwe Mulungu anamsankhira munthu wamng'ono ngati Mikaya, yemwe sankakhoza nkomwe kulowa mu chiyanjano, koma iye anabwera kumeneko ndi Mawu a Ambuye. Ndipo anati, "Kazipitani kumeneko, koma ine ndinawona Israeli akubalalika ngati nkhosa zopanda m'busa." Icho chinali chododometsa, momwe Mulungu akanayimitsira munthu wamng'ono kwambiri wosazindikirika kunja uko pakati pa gulu lonse lalikulu lotchuka la aneneri foro handiredi, a aneneri a Israeli, Aneneri achiyuda atayima pamenepo akunenera mwabodza. Kodi Mikaya anadziwa bwanji kuti iye anali kulondola? Chifukwa iye anali akuyanjana ndi Mawu. Eliya ananena zinthu zomwezo zikanadzachitika; ndipo kodi iye akanadalitsa bwanji chimene Mulungu anali atachitemberera? Icho chinali chododometsa, koma Mulungu anachipangitsa icho kufika pochitika. Ndithudi chinatero.

87 Icho chinali chododometsa; pamene mnyamata wamng'ono, wowoneka mwachikazi ali ndi zingongo seveni zatsitsi zikulendewera pamutu wake, ndipo mwinamwake chingwe cha riboni mmenemo, kwa zonse zimene ine ndikuzidziwa, ngati wachikazi wamng'ono kwambiri. Dzina lake anali Samsoni. Ndipo pamene mkango, pafupifupi mapaundi-faivi-handiredi, mwinamwake, mkango unabangula ndipo unabwera kuti udzamugwire, ndipo iye anatenga manja ake ndipo anawukhadzula mkango umenewo. Ameni. Koma penyani chimene chinachitika? Mzimu wa Ambuye unadza pa iye, poyamba.

88 Ndi chimene chimayambitsa chododometsa. Ndicho chimene. Chododometsa chonga icho chingayatse moto bwalo lino, usikuuno, ndi ulemelero wa Mulungu. Ngati chikondi cha Ambuye chitalolezedwa kuti chibwere pa anthu, ndiye iwo angapemphere. Chododometsa, ndithudi. Inde.

89 Pamene Samsoni anapha mkango umenewo, ndi manja ake chabe, anawukhadzula iwo; kamnyamata kakang'ono kwambiri, kokhala ngati kachikazi kokhala ndi mangongo seveni aang'ono atsitsi akulendewera pansi kunsana kwake.

90 Icho chinali chododometsa pamene iye anatenga fupa la nsagwada ya mphongolo ija, ndi kumenya nayo mitu ya Afilisti sauzande. Pamene, zipewa zazikulu zimenezo ndi zikhotho zazikulu zazitsulo, za mkuwa zolemera mwinamwake mapaundi handiredi, kapena pafupifupi ndi zimenezo, zishango zazikulu ndi zina zotero, mikondo, amuna-ophunzitsidwa bwino, ndi chisoti chokandapala inchi-ndi-theka, chochokera ku mkuwa, anabwera kumeneko ndi kudzawonekera, ndi nkhope zawo zokha. Ndipo Samsoni anayima pamenepo ndi fupa la chibwano cha mphongolo, chinali chitakhala kumeneko mwinamwake kwa zaka forte, fifite...[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Ku chipululu, chowuma. Chabwino, kumenyetsa kumodzi pachidutswa chachitsulo chonga chimenecho chikanaphwasula icho kukhala zidutswa mamillioni. Koma iye anayima pamenepo, ndicho chinthu chokhacho, iye anatumidwa kuti amenye ndi kulichotsapo dziko limenelo. Iye analeredwa ndi kubadwa kuti adzaphe fuko limenelo. Aleluya!

91 Ngati mpingo ukanangokhoza kuzindikira chimene inu mwabwerera kuno! Ngati mpingo wa Chipentekoste ukanangozindikira chimene inu mwadzera pano! Kodi mukuimirira chiyani? Ndi chifukwa chiyani inu munatuluka mu zinthu zimenezi ndi kudzakhala chimene inu muli?

92 Iye ankadziwa chimene iye anabadwira. Iye ankadziwa pamene iye anayima. Chinthu chimene iye anali nacho mdzanja lake sichinapange kusiyanitsa kulikonse. Iye anayima pamenepo, ndipo pamene Afilisti amenewo ankabwera, ndipo kumenya kwamphamvu kuja, kwa kamunthu kakang'ono ako kataimirira pa thanthwe, kuti kakafikire pamwamba pa mitu yawo, pamene iwo anathamangira kumeneko, iye amakhoza kugogoda mbali imodzi, ndipo wina imzakeyo. Ndipo apo panali sauzande a iwo, atagona atafa pamenepo. Icho chinali chododometsa, momwe nsagwada ya mphongoloyo inagwirizanirana pamodzi. Icho chinali chododometsa, momwe kachidutswa kakang'ono ka fupa lophwanyika kanaphwanyira zisoti za mkuwa zochindikala inchi zimenezo ndi kupha Afilisti amenewo, sauzande a iwo. Ndipo iye anayimabe pamenepo ali nalo ilo mdzanja lake, mwabwino basi monga ilo linali pamene iye analinyamula ilo. Icho chinali chododometsa. Ameni ndi ameni!

93 Iye akadali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye akadali Mulungu yemweyo, kwa munthu aliyense yemwe waitanidwa kuti adzatenge Mawu a Mulungu. Mulungu adzaima pafupi ndi iye ngati iye sakhala wamantha. Samsoni akanatha kuthamanga, koma iye sanachite zimenezo. Kulondola.

94 Icho chinali chododometsa, pamene Mulungu anamuitana Yohane Mbatizi, mwana wa wansembe, wochokera ku sukulu yaikulu ya ansembe, seminare yaikulu. Ndi chifukwa chiyani

icho sichinatsatire? Chimene, chinali mwambo kuti amuna amatsatira miyambo ya makolo awo. Bwanji, icho chinali chododometsa, pamene Mulungu anamutengera Yohane ku chipululu, kuti akamuwuze iye chimene Mesiya akanati adzakhale, kuti akamuwuze iye chimene chizindikiro cha Mesiya chiti chidzakhale, momwe iye akanati adzadziwire icho. M'malo mopita ku sukulu, kuti akaphunzire chimene Mesiya akanati adzakhale, Mulungu anamutengera iye ku chipululu kuti akamuwuze chimene Mesiya akanadzakhala. Icho chinali chododometsa ndithu, kwa anthu amenewo mu tsiku limenelo. Inde.

95 Pamene kubadwa kwa namwali kunabwera, icho chinali chododometsa; momwe kuti Mulungu, polinga kuti adzizindikiritse Yekha kwa munthu, anadzakhala munthu. Momwe kuti Mulungu, Mzimu wawukulu. . .Mulungu, kwa ine, anali kale; kunalibe ngakhale kuwala, kunalibe nyenyezi, kunalibe a—a—a—atomu, kunalibe molekyulu, pamenepo—pamenepo—pamenepo panalibe chirichonse, ndipo chirichonse chinali Mulungu. Inde, ndi momwe Iye aliri wamkulu. Iye akuchokera ku Muyaya, kudutsa Muyaya. Iye nthawizonse anali Mulungu. Iye nthawizonse adzakhala ali Mulungu. Ndipo momwe moyo wonse waukulu kwambiri unadzakhalira kakang'ono, Kanyongolosi kakang'ono mchiberekero cha mkazi, kuti atenge lamulo Lake Lomwe, kuti alipire chilango cha lamulo Lake, imfa; momwe Mulungu anawonetseredwa mu thupi, momwe Mulungu wamkulu wa Kumwamba anasinthira kupsyinjika Kwake, anabwera kuchokera kwa Mulungu, kuti adzakhale munthu, kudzera mu kubadwa kwa namwali, palibe amene angakhoze kuzilingalira zimenezo.

96 Sayansi lero siyingakhoze kukuuzani inu momwe kubadwa kwa namwali kuja kunakhalira, koma Mulungu anachita zimenezo. Iye anabwera. Palibe mmodzi anali wokhoza; aliyense anabadwa mwa kugonana. Monga wo-. . .munthu mmodzi wofanana ndi ena onsewo, palibe amene akanakhoza kumuthandiza mzakeyo. Ife tonse tinali mu vuto. Ndiyeno Mulungu Mwiniwake anabwera pansi ndipo anabadwa, osati wa Myuda, osati wa Amitundu, koma Magazi Ake anali Mulungu. Magazi amachokera mwa mwamuna. Mu chochitika ichi, anali Mulungu, Mulungu mlengi, analenga khungu la Magazi mmimba mwa Maria, ndipo anadzimangira Yekha kachisi yemwe Iyemwini anatsika pansi ndikudzakhala mmenemo.

97 "Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini." Mawu omwewo *Khristu* amatanthauza "Wodzozedwa Uyo." Oh! Iye anali Mulungu, Mulungu mu chidzalo Chake ankakhala mwa Iye. Ameni. "Ndipo mwa Iye munali chidzalo cha Umulungu mthupi." Chimenecho chinali chododometsa. Icho chinadzandimitsa anthu mu tsiku limenelo, "Inu pokhala munthu, mukudzipanga Nokha Mulungu."

Izo zikuchitabe zimenezo. Koma chimodzimodzi basi, ndi chododometsa chomwecho chikuchitidwabe. Iye anali Mulungu. Iye akadali Mulungu. Iye nthawizonse adzakhala ali Mulungu. Inde, bwana. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Inde, bwana.

98 Kubadwa kwa namwali kuja kunali chinsinsi kwa anthu, iwo sankakhoza kuzimvetsa izo, chimodzimodzi monga momwe Kubadwa kwatsopano kulipo lero. Kubadwa kwatsopano ndi chinsinsi kwa anthu. Iwo sangakhoze kumvetsa izo. Iwo samadziwa chimene iwe ukutanthauza. Iwo akupeputsa iko, ukamazibweretsa izo, amati, "Chabwino, chifukwa chakuti iwe umakhulupirira chinachake." Adierekezi amakhulupirira chinthu chomwecho, ndipo amanjenjemera. Si chimene iwe ukukhulupirira; ndi chimene Mulungu kwenikweni wachita. Kubadwa Kwatsopano ndi kubadwa. Iko kunali kwatsopano. Icho chinali chododometsa, pamene Mulungu anabweretsa Moyo watsopano kwa mtundu wa anthu. Kuzikana izo, ndiko kulekana Kwamuyaya. Kulandira izo, ndi Moyo Wamuyaya. Inu muli . . .

99 Inu muli pa maziko omwewo monga Adamu ndi Eva anali. Inu mukhoza kutenga . . . Ngati Mulungu atakuikani inu pa chinthu china chirichonse, ndiye chingakhale chosalungama kwa Adamu ndi Eva. Adamu ndi Eva aliyense, usikuuno, ali nacho chabwino ndi choyipa chayikidwa patsogolo pawo. Inu mukhoza kupanga chisankho chanu. Inu mukhoza kuwatenga Mawu a Mulungu kapena kuwasiya Mawu a Mulungu. Inu mukhoza kuwatenga Mawu a Mulungu kapena kutenga zikhulupiriro zanu zachipembedzo pa Iwo. Inu mukhoza kutenga malingaliro anu amakono a zomwe izo ziri. Inu mukhoza kubadwa mwatsopano ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, kapena mukhoza kukhala okhazikika mu mpingo, chirichonse chimene inu mukufuna mutakhala.

100 "Kwa ine kukhala ndi moyo ndi Khristu." Aleluya! Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu yemweyo amene anagwa pa Tsiku la Pentekoste, pa Mpingo Wake, monga Lawi la Moto, ndipo anadzigawa Yekha, ndi malirime ogawanika, pakati pa anthu Ake, ali pano usikuuno. Ndi Mulungu yemweyo yemwe Iye anali pamenepo, Iye ali lero, ndi Mzimu Woyera womwewo. Ine ndikudziwa kuti ndi chododometsa. Izo sizingakhoze kufotokozedwa. Kutengeka, kukuwa, kulira, ndi zina zotero, sizingakhoze kufotokozedwa, koma ndi chododometsa momwe Mulungu amachitira zimenezo. Ndi Mulungu wosawoneka akukhala mu mtima wa munthu, akudzipangitsa Yekha kuwonekera, pakuwatsimikizira Mawu Ake, kuti, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

101 Icho chinali chododometsa, pamene mwana wa a kalipentala, wa Dzina la Yesu waku Nazarete, anatenga mabisiketi asanu aang'ono ndi nsomba ziwiri, ndipo anadyetsa anthu zikwi zisanu. Ngati izo si choncho, ine ndikufuna kuti

ndimuwone winawake akuchita izo lero. Ine ndikufuna inu mundifotokozere ine mtundu wa atomu yomwe Iye anaimasula. Kodi Iye anachita chiyani? Osati nsomba yokha, koma nsombayo inamera, nsombayo inapalidwa mamba, nsombayo inali itakonzedwa, nsombayo inaphikidwa, nsombayo inali chirichonse chimene iyo inali, ndipo mkatewo unabzalidwa ndipo unamera; ndipo yonse ya iyo inalambalala, ndipo Mulungu anaisandutsa iyo kuchokera—kuchokera ku nsomba yophika kukakhala nsomba yophika. Iye ankangoiphukitsa iyo ndipo Iye ankainyema iyo, ndipo Iye ankaiphukitsa iyo ndipo Iye ankainyema iyo, ndipo Iye ankaiphukitsa iyo mpaka Iye anadyetsa zikwi zisanu. Ameni.

102 Kodi mchitidwe umenewo umatanthauza chiyani: kuyinyema iyo, kuyiphukitsa iyo; kuinyema iyo, kuibzala iyo; kuidya, kuidzala iyo? Izo zikutanthauza kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, kwanthawizonse. Iye ndi Mulungu yemweyo amene anali. Iye akadali Mkate wa Moyo kwa munthu aliyense yemwe akumva njala ndi ludzu. Simungathe kuwumaliza ubwino Wake.

103 Iwo amati, "Ife sitikusowekera zozizwitsa, sitikusowekera chododometsa."

104 Iye akuyembekezera. Ndiro dongosolo Lake. Ndicho chimene Iye ali. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye akudikirira kuti inu mufikire ndi kudzatenga gawo lanu. Kodi inu mukuchita mantha kuchita zimenezo? Kodi inu mungakonde kupita kumtsinje ndi kukadziwedzera nokha nsombayo, ndi kuyesera kuyiphika iyo ndi kuyikazinga iyo mu mtundu wina wa mafuta anyama a nkhumba kapena chinachake, kapena kodi kulibwino kuyitenga iyo momwe Mulungu akuiperekera iyo? Ingofikirani mmwamba mwa chikhulupiriro, ndi kuti, "Yesu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Ine ndikudzinenera, Ambuye, ine ndikukhulupirira mwa Inu. Ikani mkati mwanga chakudya, mphamvu, chikhulupiriro chimene ine ndikuchisowa." Penyani ndipo muwone chimene chitachitike. Ndi mtima woona, Iye adzakhutitsa njala iliyonse. Iye adzachita zimenezo.

105 Yesu anali a. . .anapanga a. . .anali ndi chododometsa, pamene Iye anadyetsa anthu faivi sauzande ndi nsomba faivi, ndi—ndipo kenako nkutengera ma basiketi awiri odzadza, kapena mabasiketi angapo, pambuyo pake.

106 Icho chinali chododometsa, pamene Munthu wa mapazi monga ine ndiri nawo ndipo inu muli nawo, pa nyanja monga Nyanja ya Michigan kunja kuno, pamene mikuntho inali ikuchitika, ndipo mafunde mwinamwake anali. . .

107 Chabwino, ngati inu munayamba mwakhalapo kumeneko ndi kuwona momwe mikuntho iyo imatsikira, iyo ikuchitabe zimenezo, kudutsa Galileya kumeneko, ndipo kumawoneka ngati mtolo pansi pa nyanja yowuma. Pamene iyo ikutsikira

pansi kudzadutsa kumeneko, mphepo zimenezo mowopsya, ndi kuyamba kusesa, ndipo mafunde oyera anaimitsa ngalawayo mpaka ziyembekezo zonse zinapita. Ndipo pa nyanja imeneyo, pamene iwo anakhala akupalasa, kuchokera ku kupalasa kuyambira pafupifupi foro koloko madzulo, ine ndingati, mpaka (wotsiriza) ulonda wachinai, cha mma firii kapena foro koloko mmawa. Iwo anali atapalasa mtunda wautali bwanji kuwoloka nyanja! Ndipo iwo anamusiya Iye tsidya linalo. Ameni.

108 Ndipo pa ulonda wachinai, apa Iye akubwera, akuyenda pa mafunde. Icho chinali chododometsa. Iye anakhoza bwanji kudzipepusa Yekha mokwanira? Iye amakhoza bwanji kumaponda pa mafunde amenewo, ndi kuponda pa funde limodzi kupita pa linalo? Mafunde aakulu awo akubwera, Iye amakhoza kupita pamwamba pa limodzi, ndipo ndithudi kutsikira pa linalo, pamwamba pomwe pa limodzi, popanda dontho la madzi pa Iye. Anabwera, akuyenda pa mafunde! Tafotokozani izo kwa ine, ndipo inu simungathe. Chinali chiyani chimenecho? Icho chinali chododometsa, mwamtheradi.

109 Icho chinali chododometsa, pamene Petro, yemwe Iye anali asanamuwonepo mmoyo Wake, dzina lake anali Simoni, anayenda mpaka mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, chifukwa m'bale wake Andreya anali atamuuza iye kuti Iye anali Mesiya. Ndipo pamene Yesu anamuyang'ana munthu ameneyo mu nkhope, kwa nthawi yoyamba imene Iye anayamba wamuwonapo iye, ndipo anati, "Dzina lako ndiwe Simoni, ndipo iwe ndiwe mwana wa Yonasi," chimenecho ndi chododometsa. Ngati si choncho, ndiwuzeni ine momwe Iye anachitira izo. Icho chinali chododometsa.

110 Chifukwa chiyani? Chifukwa, Iye ndi Mawu. Ndipo Baibulo linati, "Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndipo ozindikira maganizo ndi zamkati mwa mtima." Izo zinatsimikizira kuti Iye anali Mawu, ameni, "Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

111 Icho chinali chododometsa, pamene Filipo anapita kuzungulira phiri ndipo anamupeza Natanieli, ndipo anamubweretsanso iye mu Kukhalapo kwa Yesu, ndipo Yesu anamuuza iye kumene iye anali dzulo lake. Icho chinali chododometsa, ameni, chinasonyeza kuti Iye anali Mawu. "Taonani m'Israeli amene mwa iyeyo mulibemo chinyengo."

Anati, "Ndi liti pamene Inu munandidziwa ine, Rabbi?"

112 Iye anati, "Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe." Chododometsa. Ameni.

113 Icho chinali chododometsa, pamene wamalonda wamng'ono, wa mzinda wa Yeriko, wotsutsa wa Ambuye Yesu, anakwera mu mtengo wa mkuyu, kuti abisale, kufuna amuwone Iye akamadutsa. Ndipo pamene Yesu waku Nazarete ankabwera, akuyenda pansi mu msewu, ndipo anadzayima pansi pa

mtengowo pamene iye anali, ndipo anadzuka pamenepo ndipo anamuitana iye ndi dzina lake, "Zakeyu, tsika pansi. Ine ndikupita kwanu ndi iwe ku nkhomaliro." Chododometsa! Iye anali asanamuwonepo munthuyo, masiku onse a moyo Wake. Iye anali asanaikepo maso ake pa iye.

114 Icho chinali chododometsa, pamene mwinamwake mahandiredi angapo a anthu, inde, mwinamwake fifitini, anthu twente handiredi akutuluka mu mzinda wa Yeriko, akumuseka Iye, ndi kumuseka Iye, pamene Iye ankachoka mu mzinda madzulo amenewo, kapena mmawa umenewo, kani; pamene Iye anali kupita kunja kwa mzinda, pamene anthu anali kumuponyera Iye masamba akupysa kwambiri. Ndipo ine ndikukhoza kumumva wansembe akuti, "Heyi, iwo akundiuza ine kuti Iwe umaukitsa akufa. Heyi, Iwe mneneri, Iwe amene umadzitcha Wekha mneneri! Iwo, ife tiri nawo manda onse odzaza ndi iwo kuno, amuna basi, amuna abwino, wansembe monga ine; pita kuntunda kuno, kawadzutse iwo. Tiye tikuwone Iwe ukuwukitsa akufa." Sanamve nkomwe liwu la zomwe iwo ankanena, wina akuyamika chinthu chimodzi, ndi wina chimzake.

115 Koma kumbuyo komwe uko ku khoma, mayadi thuu handiredi ndi fifite, wopemphetsa wokalamba wosauka akunjenjemera mu kuzizira kumeneko, ndi manja ake, anati, "O Yesu, Inu Mwana wa Davide, ndichitireni ine chifundo," ndipo anamuyimitsa Iye mu njira Yake. Aleluya! Kuitana kochokera kwa Yoswa, osati patali kwambiri, osati—osati mailosi teni kuchokera pamene Iye anayima apo pomwe, anaimitsa dzuwa, tsiku lina. Koma wopemphets wosauka anaimitsa M-w-a-n-a wa Mulungu, anali mu njira Yake mwa chikhulupiriro chake, chikhulupiriro cha mtundu womwewo chimene Yoswa anali nacho. Ameni. Chifukwa, iye anadziwa, ngati Iye anali Mwana wa Davide, Iye anali Mesiya wowonetseredwa, ndipo Iye akanakhoza kumubwezera iye kupenya kwake. Chododometsa! Oh, mai! Ndithudi, icho chinali chododometsa. Inde, bwana.

116 Mulungu, icho chinali chododometsa, momwe Mulungu akanakhalira munthu, kuti afe. Mulungu, Moyo, Moyo Wamuyaya, akanakhoza kukhala Mulungu (moyo wachirengedwe) kuti adzafe, kuti adzamupulumutse munthu, kumubweretsanso iye ku Moyo Wamuyaya. Icho chinali chododometsa, momwe kuti Mulungu wamkulu yemwe anadzaza danga lonse ndi Umuyaya wonse akanakhoza kubwera pansi ndi kudzakhala munthu, ndi cholinga chakuti adzafe kuti adzapulumutse mu-. . .chirengedwe Chake Chomwe. Momwe Mulungu anakhalira mmodzi wa zolengedwa Zake Zomwe, kuti adzapulumutse, chifukwa Iye analenga thupi Lake Lomwe. Yehova Atate anadzakhala, mu chidzalo, mwa Yesu Khristu Mwana Wake. Yesu anali thupi la Mulungu. Mulungu anaimiridwa mu kachisi, thupi la Yesu Khristu, ndi momwe kuti

Mmodzi uja amene anadzaza danga lonse ndi Muyaya wonse anadzakhala Munthu mmodzi. Ameni. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Pamenepo, ndipo kuti Mulungu anakhoza kudzachita zimenezo, kuti adzafe, ndipo, oh, icho chinali chododometsa, mwa icho chokha, momwe Iye anadzipangira Yekha mwanjira imeneyo ndi cholinga choti adzazunzike imfa chifukwa cha mtundu wonse wa anthu.

117 Koma, oh, chododometsa bwanji, pamene Munthu anapachikidwa, anaphedwa, anakankhira nkondo waukulu wa Chiroma, pafupifupi mainchesi sikisi kapena eyiti mulifupi, kupyoza mu mtima Wake, ndipo Magazi ndi madzi zinatuluka. Ndipo iwo anamuchotsa Iye pa mtanda, atafa, anamukulunga Iye mu—mu nsalu, ndipo anadzamuika Iye m'manda. Iye anali atafa kwambiri mpaka kenturiyo wa Chiroma anati Iye wafa, aliyense pamenepo anati Iye wafa, mwezi unati Iye wafa, nyenyezi zinati Iye wafa, dzuwa linati Iye wafa, dziko lapansi linali ndi kudzitunduza kwamanjenje, ilo linati Iye wafa. Ndipo pa tsiku lachitatu, anakhoza kuwuka ku moyo kachiwiri, wachisavundi, ku imfa. Ndicho chododometsa. Ameni. Iye anati, "Ine ndiri nayo mphamvu yowusiya moyo Wanga pansi; Ine ndiri nayo mphamvu yowudzutsa iwo kachiwiri." Chododometsa chenicheni cha Mulungu, chiukitsiro Chake chinali.

118 Icho chinali chododometsa, cha Mulungu, pamene Yesu anasankha asodzi, osa-, . . . mmalo mwa ansembe ophunzitsidwa, kuti anyamule uthenga Wake. Zinkawoneka ngati, pamene Iye anabwera, Iye akanabwera kwa Afarisi aakulu ndi Asaduki, ndipo nkudzati, "Abale, inu ndinu anthu amene kudutsa mmibadwo mwasunga chipembedzo ichi mwaukhondo. Ine ndabwera kuti ndidzakutengeni inu tsopano. Makolo anu adzakunyadirani inu, pamene iwo akhoza kuyang'ana pansi kumadera a Kumwamba," kapena kulikonse kumene iwo anali. Ine ndikukaikira zimenezo. (Yesu anati, "Inu ndinu a atate wanu, mdierekezi.") "Ndiye kuyang'ana pansi, nkuti, 'Chabwino, ife tikhala okondwa.' Iwo akhala okondwa kudziwa izi. Ine ndabwera tsopano kuti ndidzatenge pamene inu nonse mwachipititsira icho."

119 Icho chinali chododometsa, pamene Iye anatsutsa aliyense wa iwo ndipo anawauza iwo kuti iwo anali a mdierekezi, ndipo anapita uko pa Nyanja yaku Galileya ndipo anakatola asodzi mbuli amene samadziwa nkomwe momwe angalembere dzina lawo, ndi kuwapatsa iwo mafungulo a ku Ufumu wa Kumwamba, mmalo mompatsa Kayafa, mkulu wa ansembe. Zikanatheka bwanji Munthu, kwa chipembedzo chimene chinkayesetsa, chimene iwo ankaganiza kuti chinkayesetsa, mu miyambo yawo ndi zinthu kumasunga zinthu za Mulungu, ndipo apa Iye akubwera ndi kudzasankha gulu lina kumusi pa mtsinje uko, pamene anthuwo anali ophunzitsidwa, ndi ophunzira, ndipo anadutsa mmaseminare, ndi masukulu, ndi

china chirichonse, kenako Iye nkudzabwera pamenepo ndi kudzanyalanyaza zimenezo, ndi kukatenga nsodzi mbuli ndi kumupatsa iye mafungulo a ku Ufumu? Ameni.

120 Chimene chimapangitsa chododometsa ndi pamene winawake akhulupirira Mulungu ndi kumamutenga Iye pa Mawu Ake. Mawu a Mulungu anayankhula dziko lapansi kuti likhalepo. Ndicho chinthu chomwecho chimene inu muyenera kuchikhulupirira, usikuuno, ndi Mawu olonjezedwa a Mulungu.

121 Tayang'anani pa mkazi wamng'ono wosauka uyo ataima apo pa chitsime. Iye anati, "Ife tikudziwa pamene Mesiya abwera, Iye adzatiuza ife zinthu izi." Iye anali atamuuza iye chomwe vuto lake linali. Iye anati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri. Ife tikudziwa pamene Mesiya adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu zimenezo." Penyani.

122 Mulungu akuyankhula kwa hule. Ulemelero kwa Mulungu! Mulungu akuyankhula kwa wachiwerewere, ameni, ndipo akumupempha amuthandize, "Ndibweretsere Ine akumwa." Taganizani za zimenezo. Kuyankhula za chododometsa!

123 Ndipo ndi chododometsa bwanji kuti mbewu ya Moyo Wamuyaya ija, yokonzedweratu asanaikidwe maziko a dziko lapansi, inakhoza kudzisonkhanitsa mu chinthu choterocho chonga chimenecho; mwa chilakolako cha thupi, momwe kuti mayi wachikulire wosawuka uja, mwinamwake anatembenukira pa msewu, pansi mu mtima mwake iye anakonzedweratu ku Moyo Wamuyaya.

124 Pamene Mwanawankhosa anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko lapansi, molingana ndi Baibulo, maina athu analembedwa pa Bukhu limenelo. Yesu anati, "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye, ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera." Kungomwaza Kuwala!

125 Penyani pamene Kuwala kuja kunawagunda ansembe amenewo ndi luntha lawo lonse. Chinachitika ndi chiyani? Iwo anati, "Iye ndi Belezebule, wambwebwe, mdierekezi."

126 Iye anati, "Inu ndinu a atate wanu, mdierekezi." Ndiko kumene izo zinachokera.

127 Koma pamene mkazi wamng'ono uyu, wamakhalidwe oyipa akuyankhula ndi Mulungu, ndipo mbewu yokonzedweratu iyo inakhoza bwanji kuzikika mu zoterozo—munthu woyipa ngati ameneyo? Ndi chododometsa. Koma penyani pamene Kuwala kunakhudza izo. Anati, "Ambuye, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri." Tsopano, mneneri, ndi kumene Mawu a Ambuye amabwerako, kwa mneneri, mwaona. Ndipo ilo linali tchimo lake, ndipo Iye mneneri anali nawo Mawu. Chotero iye anati, "Ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Tsopano ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, Iye adzachita zinthu izi."

Iye anati, "Ine ndine Iye, amene akuyankhula ndi iwe."

128 M'bale, iye anasiya mtsuko uwo, ndipo kutali iye anapita. Umboni wake unapulumutsa mzinda wake wa Sukari. Tsopano icho chinali chododometsa, pamene Mulungu, pamene Yesu anachita izo. Inde, bwana.

129 Icho chinali chododometsa, pamene Mulungu anaika Mzimu Wake mwa achipentekoste, asodzi osauka ndi anthu osaphunzira, m'malo mwa Kayafa wamkulu waansembe. Ndipo, oh, momwe Iye anayikira Uthenga Wake! Icho chinali chododometsa, pamene Mulungu anasankha njira imene imatchedwa "mpatuko, amisala," anthuwo ankazandima, ndi kumalumpha ndi kumapitirira, ndi kumachita ngati iwo anali amisala. Iwo anawatcha iwo "amisala." Chinali chododometsa, pamene Mulungu analambalala masunagoge akulu akulu, bwalo lalikulu la Sanhedrin ndi ansembe akulu akulu apamwamba ophunzira, ndi kunyamula gulu la mbuli, asodzi osaphunzira amene sankadziwa zochuluka kuposa kungomukhulupirira Iye ndi kutenga Mawu Ake, ndi kuwona zotsatira zake. Ndipo zinamukondweretsa Mulungu kuti alambalale chimene iwo ankachitcha chinthu choyera kwambiri pa dziko lapansi, kukatola mulu wa "zinyalala zotsika," iwo unkatchedwa, ndipo njira yomwe iwo anali kupembedzera, yotchedwa "mpatuko," kuti ayipange kukhala njira ya chipulumutso. Inde. Tsopano, izo ndi zoona, inu simungakhoze kuzikana zimenezo. Paulo anati, "Mu njira yomwe imatchedwa 'mpatuko,' ndi momwe ine ndimapembedzera Mulungu wanga, Mulungu wa makolo athu; njira yomwe imatchedwa 'mpatuko.'" Inde.

130 Icho chinali chododometsa, pamene Lawi la Moto lalikulu lija limene linatsika kuchokera Kumwamba, Mngelo wa Ambuye, Lawi la Moto linawatsogolera ana a Israeli kudutsa mchipululu. Icho chinali chododometsa, limene linayankhula ndi Mose kunja uko mu chitsamba chonyeka. Ndipo icho chinali chododometsa. Ndipo zaka eyitu handiredi kenako. . .ndipo molingana ndi Lemba, mu Yohane Woyera 8:58, ngati inu mukufuna kudziwa pamene izo ziri. Inu mukufuna kudziwa pamene izo zinayambira, poyamba, kunali Eksodo 13:31. Ndipo icho chinali chododometsa, pamene, utatha ulendo wonsewo ndi nthawi yonseyo, kuti apa Yesu ananena, kuti, "Abrahamu asanakhalepo, INE NDINE." INE NDINE ndinali mu chitsamba chonyeka moto. INE NDINE ndinali Mmodzi yemwe anayankhula kwa Mose.

131 Icho chinali chinthu chachirendo, kuti itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro, ndi Saulo, Myuda wamng'ono, wamphuno yangowe, woyipidwa, ndi wopsya mtima, ndipo anapha ena a Mpingo, pa ulendo wake wopita ku Damasiko kukawagwira anthu amenewo, ndipo kumusi uko iwo anali naye mneneri dzina lake Hananiya, ndipo anali kumeneko akulosera kwa iwo, mneneri wa Ambuye, akuwauza iwo Mawu

a Ambuye, chifukwa Iye anabwera kwa iye, ndipo pamene M'busa Ananiya anali kumusi uko akunenera, Saulo anapita kumeneko kukamugwira iye, ndipo pakati pomwe pa tsiku Lawi la Moto lomwelo lomwe linkabwera pansi ndi kumatsogolera Israeli, linamukanthira Sauli pansi, ndipo anthu onse atayima pozungulira sanakhoze kuliwona Ilo, koma Ilo linali lowala kwambiri kwa Paulo mpaka Ilo linamutongola maso ake. Ameni. Iye anachita khungu. Ilo linali lenileni kwambiri kwa iye, ndipo ena onse a iwo sankakhoza kuliwona Ilo. Ndi chododometsa. Mai! Oh!

132 Chimene chokhudzira chimodzi cha munthu mmodzi chinganene, icho chikhoka kulengeza kwa wina. Ndi chifukwa chake anthu akhoza kukhala mu—mu msonkhano, ndi kumayang'ana pa ntchito ya Ambuye, ndipo nkunyamukapo ndi kutuluka, ndi kumaiseka Iyo; ndipo winayo nkugwiritsitsa kwa Iyo, ndi mtima wawo wonse. Ndi chododometsa, momwe Mulungu angakhoze kuwapangira anthu, a thupi lomwelo. Ndi chododometsa, kuwona momwe Mulungu amachitira zimenezo, ngakhale mu tsiku lino. Izo zinali zododometsa kwa Paulo.

133 Inu mukudziwa, Paulo sanamuwone Yesu mu thupi. Iye ankayenera kuvomereza vumbulutso monga momwe Petro anachitira. Petro sanamudziwe konse Yesu mwa mawonekedwe a thupi.

Iye anati, "Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?"

134 "Ena a iwo amati, bwanji, Inu ndi 'Mose,' ndipo ena amati Ndinu 'Eliya,' ndi 'Yeremiya.'"

Iye anati, "Izo si zimene ine ndinafunsa. *Inu* mumati chiyani?"

Petro anati, "Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo."

135 Iye anati, "Wodala ndiwe, Simoni mwana wa Yonasi. Thupi ndi mwazi sizinaululire izo kwa iwe, koma Atate Anga omwe ali Kumwamba aziwululira izo. Ndipo pa thanthwe ili, Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za Gehena sizidzawulaka Iwo." Ndi zimenezotu pamenepo, chododometsa. Pamene Iye anali ataimirira pamenepo, ndipo sanamudziwe Iye mu thupi laumunthu; koma iye anamudziwa Iye mwa ntchito Zake ndi vumbulutso, anamuwona Iye akukwaniritsa ndendende chimene Lemba liri.

136 Ndiwo mtundu womwewo wa chododometsa chimene chimamubweretsa munthu kuchokera ku kachikhulupiriro kena kakale kozizira, kupita kwa Mulungu wamoyo. Ndi chododometsa, kumuwona munthu yemweyo akuwerenga Baibulo lomwelo, ndi kumalikana Ilo, pamene winayo alikhulupirira Ilo ndi kuvomereza umboni wa izo. Eya, ndi chododometsa, pamene iye angakhoze kuchiwona Icho

chikugwira ntchito pa munthu winayo, zedi iye ayenera kudziwa kuti ndi Mulungu yemweyo. Kachikhulupiriro kake ndi kolakwika, ngati kali kotsutsa. Ngati Mulungu akutsimikizira Mawu Ake, ndiye kuti kachikhulupiriro kanu ndi kolakwika. Ameni. Sizikutanthauza kukhala zamwano kwambiri, koma ndicho Choonadi, chododometsa.

137 Ine ndinati, "Mphindi sarte," ndipo ndizo ndendende zimenezo. Ine ndiri nawo pafupifupi masamba sikisi a zolemba pano panobe. Chododometsa, kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ameni, ine ndimakhulupirira mu zimenezo. Ndipo ine ndiyima.

138 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Mvetserani. Kuno nthawi ina kalelo, kumusi Kummwera, kumene ine ndinachokerako, ine ndinali ndi ayisikilimu pang'ono, tsiku lina. Wogulitsa mankhwala mzanga wakale wa ine, woyera wachikulire weniweni wobadwa mwatsopano, iye anali mwamuna weniweni. Ndinali ndisanamuwone iye kwa nthawi ndithu, ndipo ndinali ndikudutsa mzindawo, ndipo ine ndinaima kuti ndimuwone iye. Ndipo ndinawona dzina lake pamwamba apo, ndipo ndinaganiza, "Chabwino, apo, iye ali ndi bizinesi iyi kuno, ndipo wakhala kumeneko kwa zaka."

139 Ine ndinapita kumeneko, ndinakalowa mkati, ndipo apo iye anali, atakhala pamenepo, akuyang'ana pansi pa magalasi ake aang'ono, inu mukudziwa, ndi kumayang'ana pa magalasi ake aang'ono omwe analendewera pansi pa tsaya lake. Ndipo anati, "Chabwino, ngati asali M'bale Branham!" Ndipo iye anaimirira, ndipo anabwera kudzandikumbatira ine, ndi kubwera kudzandisisita ine. Anamuuza mwana wake, anati, "Pitani mukatitengereko ife wina, ayisikilimu wina." Ife tinali titayima pamenepo. "Mumwa kapu ya khofi?"

140 Ine ndinati, "Ayi, bwana. Ine ndikhoza kuyankhula nanu pafupifupi kufa, ngati iwo atandipatsa ine kapu ya khofi." Ine ndinati, "Amandipangitsa ine manjenje." Ine ndinati, "Ine ndingotenga ayisikilimu."

141 Kotero, ife tinatenga ayisikilimu wina. Ndipo—ndipo atsikana anali kumbuyo uko, ndi zina zotero, mu sitolo, ndipo tinakhala pansi ndi kukhala ndi chiyanjano chaching'ono tikudya ayisikilimu.

142 Iye anati, "M'bale Branham, ine—ine ndikufuna ndikuwuzeni inu chinachake." Anati, "ine—ine ndakhala ndikunyalanyaza pang'ono kuti ndiwauze anthu ena." Ife tinayamba kuyankhula za Ambuye ndi ubwino Wake. Ndipo munthu wachikulireyo akulira, ndipo misozi ikuyenderera pansi pamasaya ake, ndipo anati, "Ine—ine ndikufuna ndikuwuzeni inu chinachake." Anati, "Izo—izo zingawoneke zachirendo kwa—kwa inu," iye anati, "koma ine ndikukhulupirira kuti munthu ngati inu akhoza kumvetsa."

Ine ndinati, "Chabwino, pitirirani nazo, m'bale. Ndi chiyani icho?"

143 Iye anati, "Kale mu nthawi ya kupsyinjika," iye anati, "mwana wanga wa imvi apo anali mnyamata chabe." Ndipo anati, "Ife tinali pano mu—mu bizinesi iyi nthawi imeneyo," ndipo iye anati, "koma anthu anali osawuka ndipo analibe chirichonse kuti adye. Ndipo kuti apeze dongosolo, kuti akapeze mankhwala kapena chinachake, iwo ankayenera kupita ndi kukayima pa mzere."

144 Ndipo ambiri a inu mukukumbukira zimenezo. Zedi, inu mukutero. Ankaima pa mzere, kuti apeze chilolezo pang'ono kuchokera ku likuli, kuti akhoza kutenga mankhwala awa, kapena kuti atenge chinachake choti adye.

145 Ndipo iye anati, "Ine ndinakhala pano, tsiku lina, ndikuwerenga Baibulo langa, ndipo, ndipo," anati, "winawake anadzalowa pakhomo. Ndipo mwana wanga ananyamuka, wamng'ono, anapita kutsogolo." Ndipo anati, "Ind ndinamumva iye akunena kuti, 'Ayi, ife sitingachite zimenezo.'"

146 Ndipo anati, "Ine ndinamvetsera mwatcheru. Ine ndinayika Mawu anga pansi ndipo ine ndinamvetsera mwatcheru. Ndipo munthuyo anati, 'Bwana,' iye anati, 'mkazi wanga ali pafupi kuti akomoke.'" Ndipo pamene iye anayang'ana, iye anati iye anamuwona mkaziyo anali atakonzeka kuti abale mwana; banja lachinyamata. Ndipo mnyamatayo anati kwa iye, "Iye anati, 'Ine—ine—ine ndinaima pamzere umenewo uko,' anati, 'oh, wotalika ngati mdadada wa mzinda.' Ndipo anati, 'Mkazi wanga sangathenso kuimirira pamenepo.' Anati, 'Ine ndikudabwa . . . Ine ndiri ndi dongosolo kuchokera kwa adokotala, iye ayenera amwe mankhwalawo, pomwe pano.' Anati, 'Kodi inu mungalembe izo, ndipo zikatero ine ndimutengere iye kunyumba, ndipo kenako ndipita ndikayime pa mzerewo? Ine ndidza—ine ndidza—dongosolo la izo. Ngati mungatero . . .'

147 "Ndipo mwanayo anati, mnyamata anati 'Bwana, zimenezo ndi zotsemphana ndi malamulo pano. Ife, ife sitingakhoze kuchita zimenezo.'

148 "Iye anati, 'Chabwino, ine sindimadziwa.' Anati, 'Zikomo inu, kwambiri, mwana,' anatembenuka ndikuchokapo."

149 Ndipo iye anati, atangoyamba kuyenda, winawake anati kwa iye, pansi—pansi mu mtima mwake, anati, "Yosefe ndi Maria anakanidwa, nthawi ina, nawonso."

150 Ndipo anati, "Ine ndinadzuka ndipo ndinati, 'Dikira, mwana! Miniti chabe!'" Ndipo anati, "Munthuyo anaima. Ndipo ine ndinapita ndi kukatenga mankhalawo, ndipo ndinabwerera kuseri uko ndipo ndinakalemba izo; pamene iye anali akudikirira, atamugwira mkazi wake padzanja. Ndipo iye anali atafooka kwambiri, iye anali atangotsamira pa phewa lake."

151 Ndipo anati, "Ine ndinayenda kunja uko, ndipo ine. . . " Iye anati, "Pepani ine ndiyenera kuchita izi, bwana."

Iye anati, "Izo ziri bwino."

152 "Iye anali ataweramitsa mutu wake pansi, ndipo anangopereka." Ndipo pamene iye anawaika iwo mdzanja lake, iye anati, "M'bale Branham, ine ndinamuwona Yesu." Anati, "Ine ndinawaika iwo mdzanja Lake momwe." Anati, "M'bale Branham, Iye anali ali pamenepo, ndendende basi momwe chithunzicho chimawonetsera izo." Ndipo anati, "Ine—ine sindinathe kuyankhula. Ndipo mwamunayo anatembenuka pamenepo ndipo anatuluka mchipindamo."

Iye anati, "Kodi inu mukukhulupirira zimenezo, M'bale Branham?"

153 Ine ndinati, "Ine ndikukhulupirira izo ndi zonse zomwe ziri mkati mwanga. Ndithudi."

154 Martin Woyera waku Tours, ngati inu munayamba mwawerengapo za Martin Woyera, iye anali msirikali. Ndipo iye anali—iye anali wake. . .anatsatira mapazi a abambo ake. Iye nthawizonse ankamva kuyitana kwa Mulungu. Kokha, ine ndikuganiza, anthu ake sanali achipembedzo kwenikweni. Ndipo tsiku lina iye anali akubwera. . .

155 Inali nyengo yachisanu yoipa, mbiri imatero. Ndipo iye anali. . .Uko kunali wopempha-pempha wokalamba atagona panja pa chipata, ndipo iye anali akuzizidwa pafupifupi kufa; ndi anthu ambiri, amene akanatha kumudyetsa munthu wokalamba uja, kapena kumupatsa iye zovala zina. . .Iye anali akulira, atakweza dzanja lake mmwamba. Basi bambo wokalamba wandevu, wosasamba atagona pa chipata cha mu mzindawo. Ndipo iye ankati, "Ndithandizeni ine, winawake. Ine—ine ndikuzizidwa. Usikuuno ine ndifa. Winawake andipatse ine chovala."

156 Martin Woyera anali atapereka zonse zomwe iye anali nazo, anapatsa. Iye basi, monga msirikali, iye anali atavala chikhoto chake. Iye anayima cha kumbali imodzi, ndipo ankayang'ana ndi kuwona ngati winawake sakanati achite zimenezo. Anthu ankabwera ndi kumapita, ndipo palibe amene akanamuthandiza iye.

157 Kenako iye anafikira pamwamba apo, ndipo anayang'ana pa bambo wokalambayo. Iye anali ndi chifundo pa iye. Anasolola chikhoto chake chomwe, ndipo anatenga lupanga lake anachidula icho pakati. Anakulunga gawo la icho pa mapewa ake, anatenga theka linalo ndi kukamukulunga nalo wopemphetsa wokalambayo mu icho, kuchitira kuti akhale ndi moyo kudutsa usikuwo, anayamba kuyenda kumapitirira.

158 Anthu anamseka iye, anati, "Ndi msirikali wowoneka-moseketsa bwanji, atavala theka la chikhotho lokha."

159 Usiku umenewo, pamene iye anali m'tulo pa bedi, iye anadzuka. Winawake anali atalowa mchipindamo. Iye anayang'ana, atayima pachipindacho, ndipo apo panayima Yesu ndi chigamba chakale chija cha chovala chitakutiridwa pa iye. Iye anadziwa ndi zimenezo.

160 Iye anali mwamunayo, Martin Woyera, anali mmodzi wa amuna amene ankalimbanira kumbuyo uko, chifukwa cha Chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera. Iye ankakhulupirira mu zozizwitsa za Mulungu. Iye ankakhulupirira mu kuyankhula ndi malirime. Iye ankakhulupirira Chipangano chonse chimene chinalembedwa ndi atumwi. Iye ankakhulupirira ndipo ankalimbanira Icho, utali wonse iye anali ndi moyo, ndipo Mulungu ankachita zozizwitsa. Iye anadziwa, pamene iye anamuwona wopemphetsa wokalamba uja atakulungidwa mu chidutswa cha chovala cha malaya ake omwe, kuti Mawu a Mulungu anali atakwaniritsidwa, "Mochuluka monga inu mwachitira kwa aang'ono awa, Ana Anga aang'ono, inu mwchitira izo kwa Ine."

Inu mukuti, "Munthuyo sanaziwone izo."

161 Ine ndikukhulupirira iye anaziwona izo. Ine ndikukhulupirira iye analandira icho. Ine ndikukhulupirira kuti izo ziri pamenepo. Ine ndikukhulupirira uyo anali Yesu yemwe iye ankamuyang'ana. Ilo linali vumbulutso la Mulungu litawonetseredwa, chifukwa iye analichita.

162 Kukamba za chododometsa, apo pakubwera chimodzi. "Pamene akufa mwa Khristu adzauka, ndipo ife amene tiri amoyo tidzasinthidwa, mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso, kuti tidzakwatulidwe pamodzi kukakomana ndi Iye mu mlengalenga." Inde.

163 Oh, momwe Mulungu akusungira Mawu Ake mu m'badwo waluntha uno! Momwe Iye aliri yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Momwe Iye akukhozerabe kuzindikira malingaliro a mtima wa munthu! Momwe Iye angakhoze kumusintha munthu! Ndi momwe Iye angakhoze kusungabe mawu aliwonse amene Iye analonjeza mu tsiku lino! Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Momwe Iye angakhoze kuwonetserabe ndi kuwalola iwo kuti ajambule chithunzi cha Lawi la Moto lomwelo limene linkatsatira Israeli, Mmodzi yemweyo amene anali ndi Ambuye Yesu, Mmodzi yemweyo anali kumusi uko ndi Saulo panjira, Mmodzi yemweyo amene anabwera ndi kudzamumasula Petro kuchokera mu ndende! Mngelo yemweyo wa Mulungu ali pano usikuuno, ndipo akuchita chinthu chomwecho chimene Iwo anachita pamene Iwo anali kuno pa dziko lapansi akuwonetseredwa mu thupi la munthu. Chifukwa chiyani? Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

164 Kodi inu mumakhulupirira mu chododometsa? Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu akufuna kuti anthu azikhulupirira mu chododometsa. Ine ndadutsitsa nthawi yanga. Ine ndikukhulupirira icho chikhoza kukhala chododometsa pomwe pano. Ameni. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu ndi wololera ndipo akufuna kuti awatenge anthu Ake ndi kudziwonetsera Yekha. Ngati Iye atangokhoza kumutenga mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, kuti ayike pansi malingaliro awo omwe, ndi kukhala wamndende kwa Iye ndi kumukhulupirira Iye.

165 Iye ali Mawu Ake. "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu."

166 Ndipo tsopano Iye ali mwa inu, chiyembekezo cha Ulemerero, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye ananena, mu Yohane Woyera 14:12, "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita."

167 Iye analonjeza, mu Luka Woyera, kuti, "monga izo zinali mmasiku a Sodomu," pamene Mpingo wosankhidwa, Gulu la Abrahamu, lidzalandira chizindikiro monga Abrahamu analandira, ndipo gulu la Loti likanadzalandira chizindikiro monga Loti anachitira.

168 Ndi chinthu chachirendo kwambiri kuti ife takhala nawo okonzanso aakulu awa, a Luther ndi Wesley, koma ife sitinayambe takhalapo naye munthu kunja uko dzina lake likuthera mu h-a-m, mtumiki kwa dziko. G-r-a-h-a-m, ndi zilembo sikisi. A-b-r-a-h-a-m ndi Abraham. Ife takhala nawo a Moody, a Sankey, Finney, ndi Knox, Calvin, koma osati *ham*, "atate kwa amitundu." Ife tiri naye mmodzi tsopano. Ndicho chododometsa. Kodi inu mumadziwa zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndipo taonani, iye akuchita chimodzimodzi basi, kuwaitanira iwo kuti atuluke mu Sodomu.

169 Koma, kumbukirani, Abrahamu anali naye mtumiki kumeneko kwa gulu lake, nayenso. Ameni. Ndipo ndi chizindikiro cha mtundu wanji chimene Iye anachita, atatembenuzira nsana Wake ku hema? Anati, "Ine ndidzakuchezerani inu molingana ndi nthawi ya lonjezo Langa, molingana ndi nthawi ya moyo." Ndipo Iye anati, "Kodi ali kuti mkazi wako, Sarah?"

170 Anati, "Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu." Ndipo pamene iye ananena zimenezo, Sarah anaseka mwa iye yekha.

171 Iye anati, "Ndi chifukwa chiyani Sarah waseka, ndikuti, 'Zinthu zimenezi sizingakhale'?" Mukuona?

172 Yesu anati, "Monga zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu, ntchito zimene Ine ndikuchita!" Mawu a Mulungu

anadzakhala chomwecho. “Ngati inu mukhala mwa Ine, Mawu Anga akakhala mwa inu, pemphani chirichonse cha izo chimene mukufuna, ndipo chidzawonetseredwa kwa inu.” Chododometsa, kuwona lonjezo la Mulungu. . . lonjezo la Mulungu, lomwe lapangidwa kwa zaka thuu sauzande, ndipo kakhalidwe ka mpingo kawakokera anthu kutali kwambiri. Koma pakati pa izo zonse, Mulungu akubwera pansi pomwe ndi kudzawaphulitsa Mawu amenewo kubwerera mu Mpingo Wake kachiwiri, ndendende basi. Icho ndi chododometsa. Kodi inu mukumukhulupirira Iye?

Tiyeni tipemphere.

173 Ngati alipo anthu muno, usikuuno, amene angafune kuwona chododometsa chikuchitidwa pa inu, ndi kusintha mtima wanu kuchokera ku kusakhulupirira, kupita kokhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, kodi inu mungakweze manja anu, ndi kunena kuti, “Ambuye, mundikumbukire ine, mundikumbukire ine.” Mulungu akudalitseni inu. Oh, tangoyang’anani pa manjawo!

174 Atate Akumwamba, pali manja ambiri, ine sindingakhoze kunena kuti “Mulungu akudalitseni inu,” mmodzi aliyense, koma Inu mukuwadziwa iwo onse. Asintheni kuganiza kwawo, Ambuye. Oh, mulole izo zichitike, chododometsa. Iwo nthawizone amakhala ngati amapendama. Iwo amakhulupirira mwatheka, mwinamwake. Mwinamwake ena a iwo ndi a mpingo, koma komabe iwo sanakumanepo nayo nthawi imeneyo pamene iwo anakhala nawo ufulu wapamwamba, nakhulupirira, ndipo nadziwa kuti izo zimene Mulungu analonjeza, Mulungu anali wokhoza kuzichita. Komabe, ife timadzitcha kuti ndife mbewu ya Abrahamu, amene sanagwedere pa lonjezo la Mulungu mwa kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akupereka mathokozo kwa Mulungu. Tsopano, Atate Mulungu, ine ndikukupemphani Inu, mu Dzina la Yesu, kuti muwachitire iwo chifundo.

175 O Mulungu, bwerani kuno pakati pathu, usikuuno, dzayendereni pa ife ndipo mudzatisonyeze ife kuti Inu mukadali Mulungu wa zozizwitsa. Pangani chododometsa, Ambuye, ndipo mudzasonyeze kuti Mawu Anu akukhozabe kuzindikira malingaliro ndi zolinga za mu mtima. Inu mukadali Mmodzi yemweyo amene anawonetseredwa kunja uko, yemwe Abrahamu anamutcha Elohim, Ambuye Mulungu, Mlengi, Mmodzi wokwanira Muzonse, Mmodzi wokhalapo-Yekha. O Mulungu, Inu mukadali Mulungu Wamuyaya, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo Magazi a Mwana Wanu awuyeretsa Mpingo ndi kuwutsuka Iwo. Kuti, Mawu, oh, ngati iwo akanangowatenga Iwo popanda kuwonjezera kachikhulupiriro, Ambuye!

176 Koma, tsopano, Iye anati, “Ine ndine Mpesa, inu ndinu

nthambi zake. Nthambi imabala chipatso cha mpesa; pakuti moyo wa mpesa, wa nthambi, umachokera ku mpesa." Momwe ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izi, Ambuye! Momwe izo ziliri zangwiro!

177 Ndipo mu tsiku lino la kusakhulupirira ndi matsenga, ndi—ndi mitundu yonse ya tizikhulupiriro, komabe Ndinu Mulungu yemweyo amene anamuimitsira Yoswa dzuwa. Ndinu Mmodzi yemweyo amene anali pa ndodo imene Mose anaitambasula panyanja. Ndinu Mmodzi yemweyo amene amakhoza kuitanitsa nsabwe, utitiri, achule, chirichonse chimene icho chinali, mwa kamwa ya Mose. Ndinu Mulungu yemweyo yemwe anakhoza kuyika mvula mu mlengalenga. Ndinu Mmodzi yemweyo amene mudzavumbitse moto kuchokera mu mlengalenga. Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

178 O Ambuye Mulungu, tiwonetseni ife ulemelero Wanu, usikuuno, pa kumupulumutsa ndi kumudzaza munthu aliyense yemwe anakweza dzanja lake. Perekani izi, Ambuye. Mulole ilo lisangokhale pemphero lina lokhuthala. Mulole iyo isakhale njira ina yokhuthala yokwezera mmwamba dzanja lathu, pansi pa kukopa pang'ono kwa—kwa chinachake. Koma mulole izo zikhale kuchokera pansi pa mtima, kuti anthu akufulira mokweza, "O Ambuye Mulungu, lengani mwa ine chikhulupiriro chimene chingakhulupirire Inu ndi kukhoza kulandira Mawu aliwonse, ndi kuvomereza lonjezo lirilonse, ndi ameni." Perekani izi, Atate. Ine ndikuzipereka izo kwa Inu tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

179 Chabwino, ndi teni koloko. Ife sitikusowa kuti tikhale ndi mzere wa pemphero kuntunda kuno. Ife tikhoza kukhala nawo iwo kunja uko. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

180 Ndi angati muno amene akukhulupirira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, amene akukhulupirira kuti mkazi wamng'ono uja yemwe anakhudza chovala Chake ndi chala chake pamenepo, Iye anali—Iye anali mthupi, iye anakhudza chovala Chake. Apo pali chododometsa. Iye sakanakhoza kuzimverera izo, ndipo Iye anatembenuka ndipo anati, "Ndani wandikhudza Ine?" Ndipo iye sakanakhoza kuzibisa yekha. Ndipo Iye ananena za mavuto ake, ndipo chikhulupiriro chake chinamuchiritsa iye.

181 Ndipo Baibulo limanena, lero, mu Ahebri, kuti, "Iyeyo ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi zomverera za kufooka kwathu." Ndi odwala angati akukhulupirira zimenezo? Kwezani dzanja lanu. Chabwino, inu mukukhulupirira zimenezo, ndipo tiyeni tiwone tsopano ngati izo ziri zoona.

182 Inu mukuti, "M'bale Branham, izo zimabwera motani?" Kungokhulupirira Mawu basi momwe Iwo analembedwera. Osatengera zongomva zirizonse, zomwe munthu *uyu* akunena

kuti Iwo *ali* mwanjira iyi, ndipo munthu *uyu* akuti Iwo ali mwanjira *imeneyo*. Inu muwakhulupirire Iwo basi momwe Iwo analembedwera.

183 Ngati Iye ayenera kuti adzakuweruzeni inu monga momwe Iwo analembedwera, ndiye bwanji kutenga kutanthauzira kwa winawake kwa Iwo, chifukwa umo ndi momwe iwo ati adzawerudzidwire. Mmenemo basi, Ndiwo muyezo Wake. Iye wawayang'anira Mawu Ake. Palibe cholakwika ndi izo. Ndizo ndendende basi Mawu. Ndicho chimene ife titi tidzaweruzidwe nacho, ndi Ichi, ndi Mawu a Mulungu.

184 "Ndipo ngati inu mukhala mwa Ine," ndicho chikhulupiriro, "Mawu Anga akakhala mwa inu," chifukwa Iye ali Mawu, "ndiye mupemphe chimene inu mukufuna."

185 Tsopano inu mukhudze chovala Chake, kuti, "Ambuye Yesu, ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti ife tikukhala mmasiku otsiriza. Ine ndikukhulupirira Inu ndinu Mulungu yemweyo amene munachita zozizwitsa zonse izi zimene abusa athu atisonyeza ife, usikuuno, mu Mawu. Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndinu Wansembe Wamkulu. Ambuye, mundirole ine ndikhudze chovala Chanu. Ndiye Inu muyankhule kupyolera mwa m'bale uyu, ndipo—ndipo akudzinenera kuti Inu mumayankhula kupyolera mwa iye. Ndipo, ndiye, iye sakundidziwa ine, koma Inu mukundidziwa ine." Ndiyeno muwone ngati Iye sali Mulungu yemweyo wa zozizwitsa, ndipo pakhala chododometsa kachiwiri, chinthu chosafufuzidwa chimene munthu sangakhoze kuchizindikira ndi kuchinena.

186 Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ngati Iye ati achita zimenezo, ndiye ife tikudziwa kuti icho chikhala chododometsa. Nkulondola uko? Ine ndimati ndikhale ndi mzere wa pemphero; ine ndinangotengeka nazo kwambiri mpaka ine—ine—ine ndangochokako kwa izo, ndipo nthawi yapita. Inu mukhulupirire. Tiyeni tiyambirenso . . . ine sindingathe . . .

187 Ine ndiyenera kukulekanitsani inu. Tiyeni tiyambire mbali *iyi* apa. Winawake mwa njira *iyi*. Ndi angati cha *apa* akudziwa kuti ine sindikukudziwani inu kapena ine sindikudziwa kanthu za inu, kwezani mmwamba manja anu; ndipo inu mukudwala, inu mukudziwa kuti inu mukufuna kumupempha Mulungu? Chabwino.

188 Ena a inu mukukhulupirira, basi—basi ingotengani izi ndi mtima wanu wonse. "Ambuye Yesu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Ndiroleni ine ndikukhudzeni Inu, Ambuye. Chikhulupiriro changa chikusunthira kwa Inu kutsidyako pa dzanja lamanja la Mulungu, mutakhala mu Ufumu. Ndipo Mzimu Wanu Woyera, umene unali mwa Inu, uli pano usikuuno. Ndiroleni ine ndingokhudza, mwa chikhulupiriro, Ambuye." Ndiye muwone ngati Iye akadali mwini wa chododometsa,

kubweretsa zinthu zomwe ziri zosadziwika mwamtheradi. Mungokhala molemekeza.

189 Apa, mukuwona izi pomwe apa? Ndi dona wachikuda wakhala kumbuyo komwe kuno. Iye akuvutitsidwa ndi vuto la impsyo. Iye wangokhala kumene ndi opareshoni. Ine sindikumudziwa donayu.

190 Ndine mlendo kwa inu. Nkulondola uko, dona? Koma izo ndizoona, sichoncho izo? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu yemweyo yemwe anakhoza kumuuza mkazi wamng'ono uja yemwe anakhudza chovala Chake uko, ndi—ndipo tsidya lina la nyanja, kodi inu mukukhulupirira kuti ameneyo ndi Mulungu yemweyo? Inu simungakhoze kundikhudza ine, mwathupi, inu mukudziwa. Kotero ine basi . . . Ndipo ine sindikukudziwani inu. Kotero pali Wansembe Wamkulu, chifukwa Iye anati Iye anali Wansembe Wamkulu. Nkulondola uko? Ndipo inu mukukhulupirira zimenezo. Pamene inu munali pamenepo mukupempherera kuti mukhale inu, chinachake chinakukhudzani inu, ndipo nthawi yomweyo ine ndinatchula za icho. Nkulondola uko? Chabwino.

191 Opareshoni yomwe inu munali nayo sinawoneke kukhala yopambana kwambiri. Inu simukupeza bwino, inunso, ndipo mukuchita nazo mantha zimenezo. Ndipo inu mwabwera kuno usikuuno kwa cholinga chomwecho. Ngati Ambuye Yesu ati awulule kwa ine yemwe inu muli, monga Iye anachitira Simoni amene anabwera uko, kodi inu mungandikhulupirire ine kuti ndine mneneri Wake, wantchito Wake? Inu mukukhulupirira zimenezo? Akazi a Pigrum. Ndiko kulondola. Tsopano inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu pitani kwanu ndipo mukakhale bwino. Inu mukakhala bwino chifukwa chikhulupiriro chanu chakuchizani inu.

192 Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Nanga bwanji chigawo *ichi* chomwe chiri muno, kwinakwake, winawake akukhulupirira?

193 Mwamuna wakhala kunja kuno kumapeto, iye akuvutika ndi vuto ndi maso ake. Ine sindikudziwa ngati iye akudziwa . . . Inde, iye wandigwira ine tsopano. Iye akuwumverera Mzimu. Inde, kodi inu mukukuwona Kuwala kuja pamwamba pa munthuyo? Bambo Otis, limenelo ndiro dzina lanu. Ndine mlendo kwathunthu kwa inu, koma inu mukudandaula za maso anu. Khristu akuchiritsani inu, chikhulupiriro chanu.

194 Tsopano mufunseni mwamunayo ngati ine ndinayamba ndamuwonapo iye, kudziwa chirichonse za iye, kapena mkazi uyu, kapena kulikonse kumene kuli. Ndi chimenecho chododometsa. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Iye ali yemweyo dzulo, lero. Iye analonjeza, "Ntchito zimene Ine ndikuzichita, inunso mudzazichita." Umo ndi momwe Iye anadzizindikiritsira Yekha kuti ndi Mesiya. Nkulondola uko?

Chabwino, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo inu mukudziwa kuti uyo sangakhale ine. Ine sindine Mesiya. Ndine munnthu chabe, m'bale wanu. Koma ndi Mzimu Woyera pano, ameneyo ndi Mesiya. Ndiye Mtsogoleriyo. Iye ndi Yemwe akudziwa. Ine sindikuwadziwa anthu amenewo; iwo akudziwa zimenezo.

195 Pano, ine ndikufuna ndikuwonetseni inu. Pali mkazi wachikuda wakhala apo pomwe pambali, pamwamba apo, akuvutika ndi vuto la chithokomiro. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Akazi a Kelly. [Mlongo akulira, "Ameneyo Ndine!"—Mkonzi]. Ndiko kulondola. Chabwino.

196 Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse?

197 Bambo Swanson kumbuyo uko, ndi vuto lamanjenje, kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukupangani inu kukhala bwino? Ngati inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse! Chabwino, inu mukhoza kukhala nacho icho. Mulungu wakuchiritsani inu.

198 Kodi inu mukukhulupirira izo? Ine sindikuwadziwa anthu amenewo. Afunseni iwo ngati ine ndikuwadziwa iwo. Ndi chododometsa.

199 Miniti yokha. Apa pali Kuwala uku, Iko kwayima pa mkazi. Ine ndikudziwa yemwe iye ali. Iye wakhala pomwe pano. Musati mudandaule, Akazi a Collins, lekani kuvutikira nazo izo, kudzipangitsa nokha kudwala. Izo zonse zituluka bwino bwino. Mulungu amatsogolera. Tsopano, ine ndikumudziwa mkazi ameneyo. Ine ndikumudziwa yemwe iye ali. Iye ndi wochokera uko ku Indiana, kapena Kentucky. Ine ndikumudziwa iye. Mwamuna wake kumeneko, ndi membala wa mpingo wanga, iye ndi—iye ndi dikoni kumusi uko, mwamuna wabwino. Koma ndi uko Kuwala kuja. Kodi inu simukukuwona Iko pomwepo pa iye? Iye wakhala akuvutitsidwa, iye akudwala, ndipo iye wakhumudwa ndi chinachake chimene iye sakudziwa kuti achite kapena ayi. Inu mungokumbukira, lekani kukhumudwa, mlongo, izo zikhala bwino. Iye amadziwa zonse za izo. Iye akutsogolerani ngati inu mumusiye Iye atero.

200 Ameni! Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Iye ndi chododometsa! Ndife oyamikira chifukwa cha izo. Kodi inu mukukhulupirira izo?

201 Imiririrani pamapazi anu ndiye ndi kuvomereza izo, ndikuti, "Ambuye Mulungu, ine ndikubwera kwa Inu mu Dzina la Yesu Khristu, chitani mwa ine, ndipo mubweretse ulemelero ndi madalitso Anu ndi mphamvu pa ine. Mulole mubwere chododometsa mu mtima mwanga pakali pano. Ine ndikukhulupirira. Ine ndikukhulupirira." Ndi mtima wanu wonse, khulupiririrani izo.

202 Kwezani manja anu pamene inu mukuyimba nyimbo yakale iyi, “Ine ndinkonda Iye, ine ndinkonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine.” Tsekani maso anu. Tsekani maganizo anu onse, ndipo mungomulola Yesu Khristu abwere mwa inu, ndipo aliyense wa inu achiritsidwa ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.

203 Chododometsa chimodzi, usikuuno, chingawaike ano, chiyenera kuwayatsa malo ano. Yesu Khristu ali pano. Ndani angafotokoze zimenezo? Afunseni anthu awa, pitani kwa iwo. Inu muli nawo maina awo ndi zinthu, pa tepi iyi. Pitani, kawafunseni iwo. Mwaona, ine sindikudziwa kanthu za iwo. Icho chimachita chiyani? Mulungu, mu m’badwo waluntha uno. . .

204 “Ili kuti mvula iliyonse mlengalenga” anatero wasayansi mu tsiku la Nowa, “ili kuti iyo mmwamba umo?” Mulungu analonjeza izo! Iyo ibwera.

205 Kodi zinthu zimenezi zingatheke bwanji? Ine sindikudziwa. Mulungu analonjeza izo! Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Aleluya! Chododometsa! Ine ndimkonda Iye, ine ndimkonda Iye, chifukwa Iye anayamba kundikonda ine, ndipo watsegula maso anga akhungu, kuti ine ndikhoze kubwera mkati ndi kudzawona Kukhalapo Kwake ndi kudziwa kuti Iye ali pano. Ameni ndi ameni!

206 Tiyeni tingokweza manja athu ndi kumupembedza Iye tsopano pamene ife tikuyimba iyo. Ulemelero kwa Mulungu! Mathokozo akhale kwa Ambuye Yesu Khristu, chifukwa cha ubwino Wake ndi chifundo! Mulungu akudalitseni inu.

63-0801 Chododometsa
Marigold Center
Chicago, Illinois U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org